


AHEBRI, MUTU

WACHISANU NDIPONSO

WACHISANU NDI CHIMODZI ¹

 ...wa—wa Bukhu la Ahebri. Ndiye ife tilowa mu wa 7, unsembe wa Melkizedeki. Ndiyeno ife tidzalowa mu, kuchokera ku unsembe wa Melkizedeki, kukalowa mu masiku aakulu aja a chitetezero, ndi kulekanitsa, kugawaniza zitetezero. Ndiye kulowa mu mutu wa chikhulupiriro chachikulu uja, mutu wa 11. Ndi mutu wa 12, “Kuika kumbali cholemera chirichonse.” Ndi mutu wa 13, “Kwathu Kwamuyaya kuja kosamangidwa ndi manja a munthu; koma Mulungu, yekha, yemwe anapanga kwathu kwakukulu uku.” Kudabwitsa kwakeko!

² Ndine wokondwa kumuwona mlongo wathu kumbuyo uko, yemwe wangolowa kumene mu msonkhano. Ine ndikumuwona iye ndi mwamuma wake. Dzulo, ife tinali panjira yathu chokwera, tikudutsa pamalo omwe... Ine ndinkaganiza kuti ine ndinkadziwa mng'aru waung'ono uliwonse ndi pokhota, pokhala woyang'anira zinyama kuno mu Indiana, ndi wolondera kwa zaka zambiri. Ine ndinkadziwa malo aliwonse. Koma ine ndikanati ndisochere dzulo, kumeneko komwe iwo anali, pamwamba pa magomo, msewu watsopano.

³ Ndipo donayo anali ndi khansara mu mapapo, ndipo Ambuye motsimikizika anamuchiza mkaziyo. Ife tinatenga... O, ndipo momwe zonsezo zinadzera, ife tinali titakhala pamenepo. M'bale Roberson, iye mwinamwake ali muno, lero. Ine ndikumuwona mkazi wake, ndi M'bale Woods, omwe ali muno. Ndipo ife tinali kumeneko mu chigalimoto chakale, M'bale Roberson ndi ine, ndi M'bale Woods. Ndipo ife tinatenga galimoto iyi, tinapita pamwamba apo, pamwamba pa phiri. Ndipo apo Ambuye anasonyeza khansarayo motsimikizika. Ndiyeno ife tinaima apo ndipo tinaiwona iyo ikumusiya mkaziyo. Ndi maso athu omwe, ife tinaima ndi kumaiyang'ana iyo ikumusiya mkaziyo. Ndipo iye anaitananso kwa akazi a M'bale Wood; ndipo amandiuza ine, iye anali akulavula zinthu zakuda kwenikweni zija. Ndipo ndi uyo apa mmawa uno, wakhala mmbuyo mwa kachisiyu, iyeyo ndi mwamuna wake wokonedwa, ali ndi nthawi yodabwitsa mwa Ambuye. Kodi Iye si wodabwitsa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

⁴ Ndipo ine sindinali kudziwa kuti... Apa, kawirikawiri, kwa anthu omwe ali pozungulira, mwapatali patali masomphenya

amachitika kuno. Kuno ndi kwathu. Ndipo, ine ndikutanthauza, mu mpingo.

⁵ Lamlungu, sabata, ife...Ndi angati anali pano kuti anamuwona bambo wa mu chikuku? Wakhungu, wolumala, wosatha kuima, ndipo misempha ya mu ubongo itapita, ndipo a Mayo anali atamulephera iye. N—ndipo dotolo wina wa Chikatolika mzanga wa ine anamutumiza iye kuno. Ndipo ndisanabwere ku msonkhano, Ambuye anandipatsa masomphenya a bamboyo. Inu nonse mukuzidziwa zimenezo. Ndipo apo bamboyo anachizidwa, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Ndiyeno anadzukapo, nkumayenda akutuluka, atatenga chikuku chake, akukhoza kumapenya monga inu mukukhozera kapena ine ndikukhozera. Ndipo anatuluka mchiphindamo akukankha mpando wakewo, mwabwinobwino. Ndipo msempha womuimitsa...Inu mukudziwa, iwe sungakhoze kudziyimika wekha apo. Mukuona, iwe sungathe basi. Ndipo kwa zaka zakhala ziri choncho.

⁶ Ndipo dzulo pamene ine ndinafika uko, donayo anakhala ali ndi loto la kundiwona ine ndikubwera umo, basi pa thuu koloko, ndi kumuuzwa iye “kuti ali ndi khansara,” ndipo kenako, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘iye anachizidwa.’” N—ndipo iye anadzuka apo, ndipo iyo inali ndendende basi thuu koloko. Ndipo Mzimu wa Ambuye unabwera pansu, ndipo apo—loto lija lomwe iye anali nalo, ndipo Ambuye anapereka kutanthauzira. Ndipo iye anachizidwa apo pomwe pa malopo, apo pomwe pamene ife timazipenya. Kudabwitsa kwakeko!

⁷ Sindikukhoza kuganizira dzina lake. Nchiani ilo? Dzina lanu ndi ndani, mlongo? Walton, Mlongo Walton, wakhala kumbuyo ukoyo. Kodi inu mungaime apo, Mlongo Walton? Ndikufuna kuti ndikufunensi inu momwe inu mukumverera. [Mlongo Walton akuti, “Ndi zodabwitsa basi.”—Mkonzi.] Ameni. Ndizo zabwino, wabwino ndi wamphamvu. Iye ndi wabwino kwambiri, kuti akutidalitsa ife moteromo. Chotero ife tikuyembekezera zopitirira, zochulukira, za muyezeo waukulu wa Mulungu.

⁸ Adokotala anali kubisila izi kwa iye. Iwo anamuuzwa iye kuti “iye anali akungopuma kuchokera ku mbali imodzi.” Chomwe izo zinali, khansara inali itamela chodutsa ndipo inali itadula kupuma kwa kumbali iyo ya phapo, inu mukuona. Inu simungakhoze kuiwona khansara kupyolera mu x-ray, chifukwa khansara ndi khungu, payokha, ndipo iyo—ndi moyo. Ndipo i...Inu basi—inu mumakhoza kumangoyang’ana kudutsa mu khansarayo, ndi x-ray. Inu simungaiwone iyo.

⁹ Ndipo, koma Ambuye achita kwenikweni...Ife tinaima pamenepo ndipo tinaiwona iyo, ifeni, ndi maso athu omwe. Tinaiwona iyo ikusuntha, ndipo tinaiwona iyo ikuchoka, ndi maso athu omwe. Chotero, ndife oyamikira kwambiri pa izo.

¹⁰ Ndipo tsopano, zitipemphererani ife tsopano, sabata ino, pamene ife tikhala titapita. Ndipo M'bale Neville mwinamwake adzayambira pamene ine ndinalekezera, kwa ulaliki wa Lachitatu usiku. Musati mudzaphonye izo tsopano, mu kulumikizana kwakukulu uku kwa Bukhu la Chivumbulutso.

¹¹ Ine ndikudziwa kuti mapemphero ochuluka aperekedwa, ndipo i—ife tikudziwa kuti Mulungu amamva mapemphero. Koma ife, mmawa uno, ife tikufuna kuti tipereke pemphero laling'ono lokha tisanafike kukuwerenga kwa Bukhu. Tsopano, munthu aliyense yemwe ali wokhoza, angathe kuwerenga Bukhuli mwanjira *iyi*, kapena akhoza kulitsegula ilo mwanjira *iyi*. Koma izo zimatengera Mulungu, yekha, kuti atsegule kumvetsa, pakuti Iye ali Mmodzi yekha yemwe angakhoze kuchita izo.

Chotero tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi yokha.

¹² Tsopano, Atate, mu Dzina la Mwana Wanu Wokondedwa, Ambuye Yesu, ife modzichepetsa kwambiri tikubwera tsopano kuti tidzipereke tokha, monga antchito Anu, kuti Inu mungoti muyankhule kupyolera mwa ife. Pangani mdulidwe wa milomo yomwe ikuyankhula ndi makutu omwe akumvetsera, kuti Mawu akhoze kuyankhulidwa ndi Mulungu ndi kumvetsa ndi Mzimu, mwa anthu. Perekani izi, Atate. Mulole Iye atenge Mawu a Mulungu ndi kuwatumikira iwo kwa ife momwe ife tiriri ndi chosowa, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake ndi kwa ulemerero Wake. Amenii.

¹³ Tsopano, powerenga mmawa uno, ife tikuphunzira. Ife si—sitikulalikirira; tikungophunzira Bukhu ili la Ahebri. Ndi angati akukomedwa nalo ilo? O, ife tikukhala ndi nthawi yodabwitsa! Ndipo tsopano tikungophunzira mwacheru, Lemba pa Lemba. Izo ziyenera... Baibulo lamphumphu, lonselo likumangirizana palimodzi. Palibe Mawu amodzi omwe sali pa malo Ake, ngati Iwo ali ataikidwa pamodzi ndi Mzimu Woyera.

¹⁴ Tsopano, munthu ananapo kuti, “Baibulo limadzitsutsa llokha.” Ine ndikufuna kuti ndiziwone izo. Ine ndafunsapo, zaka twente faifi, izo, ndipo palibe yemwe anayamba wandisonyezapo izo panobe. Baibulo silimadzitsutsa ayi. Ngati ilo liri, ilo si Baibulo. Yehova wamkulu, wopanda malire sangakhoze kudzitsutsa Iye mwini Yekha, chotero mulibe kutsutsana mu Baibulo. Ndi kusamvetsa chabe kwa anthu.

¹⁵ Tsopano kwa maziko pang'ono, mpaka ife tibwerere mmbuyo. Tsopano, Bukhu la Ahebri linalembedwa ndi Paulo Woyera, kwa Ahebri. Iye analembera ina kwa Aefeso, amenewo anali anthu aku Efeso, Mpingo wa Chikhristu; ina kwa Achiroma ku Roma; ndipo ina kwa Agalatia; ndi ina kwa Ahebri.

¹⁶ Tsopano, ife tikuzindikira kuti Paulo, pokhala mphunzitsi wa Baibulo, pa kuyamba pomwe. Ndi zomwe ife tinaphunzira. Kuti iye anakhala pansu pa mphunzitsi wamkulu, mmodzi wa

aakulu a masiku ake, Gamaliele. Ndipo iye anali wodziwa bwino za mu Chipangano Chakale. Iye ankachidziwa icho bwino. Koma anakhala wozunza wa njira yomwe inali Njira ya Khristu, chifukwa iye anali ataphunzitsidwa za mu Chipangano Chakale pansi pa aphunzitsi. Koma aphunzitsi, kawirikawiri mwachithupithupi...ine ndikuyembekeza ine sindinena chirichonse molakwika.

¹⁷ Koma, kawirikawiri, ngati munthu angokhala ndi kuphunzitsa ndi njira ya sukulu, izo kawirikawiri zimakhala zopangidwa ndi anthu. Mukuona, izo sizimakhala zodzozedwa, chifukwa izo zimakhala chiphunzitso cha sukulu. Ife tiri nazo izo lero. Achipresbateria, Achilutera, Achipentekoste, masukulu onse awa ali nawo malingaliro awo, ndipo iwo amangotsirizitsira Malemba mu izi.

¹⁸ Ndipo izo zinali chimodzimodzi mu Chipangano Chakale. Koma, Paulo, pokhala wophunzitsidwa bwino, ndi powadziwa Malemba mwa mawu. Koma, inu mukuona, Malemba, ziribe kanthu momwe inu mukuwadziwira bwino iwo, ngati Mzimu suwafulumizitsa iwo, ndiye lembalo limapha. Mzimu umapereka Moyo. Mukuona, iwo amayenera kuti afulumizitsidwe, kapena kupangidwa amoyo, mwa Mzimu. Ngati Mzimu suwafulumizitsa Mawu ndi kuwapanga Iwo chenicheni kwa inu, ndiye lembalo ndi laluntha chabe. Ndi pamene ife timakhala ndi Akhristu ambiri odzinenera lero, kapena Akhristu odzinenera, ndi lingaliro laluntha ilo la Khristu.

¹⁹ Ndiye ife timasocherera pa, “Chabwino, iye amayenera kuti amverere chinachake; ndipo iwe umayenera kuti uchite chinachake.” Ndipo, o, ife tilowa mu zonse izo, pakapita kanthawi. Wina ankayenera kuti azifuula. Achimethodisti ankayenera kuti achite kufuula, asanakhale nacho icho. Achipentekoste ankayenera kuyankhula ndi malirime, iwo asanakhale nacho icho. Ndipo, o, ena a iwo, Odzigwedeza, ankayenera kuti azigwedezeka. Eya. Akale...Iwo ankayenda chokwera-ndi-chotsika, amuna mbali imodzi, akazi inayo. Mukuona? Odzigwedeza. Ndiye Mzimu Woyera unkabwera pa iwo ndipo unkawagwedeza iwo. “Iwo anali nawo Iwo.” Koma zonse izo ndi kutengeka basi. Palibe chirichonse cha izo chiri Choonadi.

²⁰ Mulungu amakhala mu Mawu Ake. “Chikhulupiriro chimadza pa kumva, kumva Mawu. “Mwa chikhulupiriro inu mumapulumsidwa, kudzera mu chisomo.” Osati mwa chirichonse, kaya inu mugwedezeka, kapena muyankhula ndi malirime, kapena chirichonse chomwe chingachitike. Izo ziribe kanthu kochita mu izo, konse. Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya. Iye amene amva Mawu Anga nakhulupirira, kukhala atafulumizitsidwira kwa iye, ali

nawo Moyo Wamuyaya.” Ndi izo apo. Ziribe kanthu kanthu kakang’ono komwe inu muchita.

²¹ Tsopano, ine sindikutsutsana ndi kugwedezeke, kapena kuyankhula ndi malirime, kapena kugwedezeke, o, izo—kufuula uko. Izo zonse nzabwino. Ndi zabwino. Koma ndi zotsatira chabe. Mukuona? Ine ndikhoza kukupatsani inu apulo kuchokera mu mtengo, ndipo inu mukanakhalabe mulibe mtengowo. Mukuona? Inu . . . Ndi zotsatira.

²² Kunama, kuba, kumwa, kusuta, kuchita njuga, kuchita chigololo, sindizo tchimo, ndizo zotsatira basi za kusakhulupirira. Mukuona? Ndizo zomwe i—inu. . . Inu mumachita izo chifukwa ndinu wochimwa. Mukuona? Koma poyamba ndinu wochimwa. Ndizo zomwe zimakupangitsani inu kuchita zimenezo, chifukwa inu simumakhulupirira. Ndipo ngati inu muli kukhulupirira, ndiye inu simumachitanso zimenezo. Ndiye inu mumakhala ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira, ubwino, unjonda, kufatsa, chipiriro. Ndicho chipatso cha Mzimu Woyera. Mukuona?

²³ Chotero ife tiri nazo zinthu zazing’ono, kumverera pang’ono, ndi chifukwa chakuti munthu anachoka pa njira yakale yopunthidwa, ya Mawu. Ndi Mawu. “Chikhulupiriro chimadza pa kumva.”

²⁴ Chotero pamene Paulo. . . Mulungu anamusankha Paulo. Anthu anasankha Matiya. Pamene iye . . . Iwo anapanga maere, koma iye sanachite kanthu kalikonse. Izo zikusonyeza mphamvu yomwe mpingo uli nayo ndiye, pakupanga kusankha, kuti asankhe madikoni awo, ndi kutumiza alaliki awo ku malo osiyana. Zimakhala zachithupithupi, nthawi zambiri.

²⁵ Muloleni munthu azipita kumene Mulungu amutsogolere iye kuti apite. Ine ndimakonda choncho. Ngati anthu mu msonkhano angati, “Chabwino, ichi ndi tchalitchi chabwino. M’bale uyu wamanga tchalitchi chabwino. Ndipo ife tiri ndi womuweta wamng’ono.” Iwo amutumiza iye ku mpingo uwu. Iwo sakudziwa kuti iwo akudzipha okha. Mukuona? Malo oyamba, ngati munthu ameneyo apita uko, iye sangakhoze kutenga malo a munthu ameneyo. Ndiye iwo amangowufooketsa mpingowo, pakuyesera kusonyeza kukondera kwa womuweta wina. Izo nthawizonse zakhala ziri mwanjira imeneyo.

²⁶ Koma ine ndimakhulupirira mu ulamuliro wapamwamba wa gulu wamba. Inde. Uloleni mpingo uliwose uzikhala wapa wokha, uzisankha abusa ake, madikoni ake, zake, chirichonse chomwe chiri. Ndiyeno, mwanjira imeneyo, munthu wa mmenemo samakhala ndi bishopu pamwamba pa iye. Mzimu Woyera ukafuna kuti uyankhule chinachake kwa mpingo umenewo, iwo samasowa kuti azikamufunsa aliyense ngati iwo angachite *izi* kapena kuchita *izo*. Ndi munthu aliyense payekha mwa kulumikizana ndi Mzimu Woyera. Ndisonyezeni ine mu

Baibulo yemwe ali wamkulupo, mu Baibulo, kuposa mkulu wamba kwa mpingo wamba? Ndiko kulondola, inde, bwana, kuchita kwa pawokha kwa mpingo wamba, mpingo uliwonse pawokha. Tsopano, ubale, izo ndi zodabwitsa. Mipingo yonse iyenera kuti izikhala mu ubale monga chomwecho, palimodzi. Koma kuchita kwa pawokha kwa mpingo wamba!

²⁷ Zindikirani Paulo, pokhala mphunzitsi wamkulu, wophunzitsidwa bwino, ali panjira waku Damasiko, tsiku lina, kuti akawamange anthu omwe anali mu Njira yatsopano iyi. Tsopano, iye anali wodzipereka. Mulungu samakuweruza iwe ndi kudzipereka kwako. Ine sindinayambe ndawawonapo anthu odzipereka kwambiri kuposa achikunja. Ambiri a iwo amapha ngakhale ana awo omwe, mwachabe, k—kuti achitire nsembe kwa fano. Si kudzipereka ayi. Munthu akhoza kumwa karboliki asidi, modzipereka, akuganiza kuti akumwa chinachakenso. Kudzipereka sikumakupulumutsani inu. “Ilipo njira yomwe imawoneka yolondola kwa munthu, koma mapeto ake ndi njira za imfa.”

Paulo anali wodzipereka pamene iye ankaperekerera umboni, mwa ulamuliro wake womwe, kuti amugende Stefano. Kenako mu zaka, ine ndimakonda kupepesa kwa Paulo, iye anati, “Ine sindiri woyenera kuti ndizitchedwa wophunzira kapena kuti ndizitchedwa mtumwi, chifukwa ine ndinawuzunza Mpingo mpaka ku imfa.” Ndi kudzipereka!

²⁸ Ndipo ali panjira yake akupita, iye anakomana ndi chomuchitikira. Mzimu Woyera unatulukira apo mwa Lawi la Moto lalikulu, ndipo Ilo linamuchititsa iye khungu. Tsopano, ife tinadutsa mu zimenezo, Lawi la Moto ilo linali Khristu. Ndipo Iye ali Lawi la Moto lomwelo limene linkawatsogolera ana kudutsa mchikululu. Khristu anali Mulungu, ndipo Mulungu anali Khristu. Mulungu anapangidwa thupi ndipo ankakhala mu thupi la Ambuye Yesu. “Mulungu anali mwa Khristu, akuyanjanitsa dziko kwa Iyemwini,” kusonyeza chimene Iye anali.

²⁹ Mu Baibulo kumbuyo uko, mu ndime zoyambirira zomwe ife takhala tikuziwerenga, kuti, “Iye anadzipanga Iyemwini motsikirapo kuposa Angelo. Anadzitengera mawonekedwe, osati a Angelo, koma anadzitengera mawonekedwe a mnofu.” Angelo anali asanagwe, iwo sankasowa chiwombolo. Mnofu unali utagwa, anthu okhalapo, ndipo iwo ankasowa chiwombolo. Kotero, mu malamulo akale, munthu, kuti akhale—woombola, choyamba iye ankayenera kuti akhale wapachibale; Bukhu lalikulu la Rute, ife tinadutsamo kuno, nthawiina pakalepo. Ndi momwe kuti Mulungu, pokhala Mzimu, anapangidwa wachibale limodzi nafe, pakukhala mmodzi wa ife, polinga kuti atiwobole ife ndi kutipatsa ife Moyo Wamuyaya. Iye anachita kukhala ife, kuti ife kupyolera mchisomo tikhoze kukhala monga Iye.

³⁰ Ndipo ife tikupeza Lawi la Moto linkatsogolera ana Israeli. Ndipo pamene Ilo linapangidwa thupi kuno padziko lapansi, ife tinamumva Iye akuyankhula tsiku lina, ndipo Iye anadzinenera kuti Iye anali Lawi la Motolo. Iwo anati, “Iwe ukuti ndiwe wamkulu kuposa atate athu Abrahamu?”

³¹ Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.” Nndani anali INE NDINE? Lawi la Moto mu chisamba choyaka, chikumbutso chopitirira kudutsa mu kam’badwo kalikonse; osati kokha kam’badwo ako, koma kam’badwo kano, Lawi la Moto lomwelo. Ndipo ndife othokoza kwambiri mmawa uno kuti ife tiri nacho ngakhale chithunzi cha Ilo, kuti Iye sanasinthe. Iye ndi Wachisavundi, Wamuyaya, Mmodzi Wodalayo. Iye akuchita zinthu zomwezo tsopano zimene Iye ankazichita apo, ndipo momwe izo zikutipangitsira ife kumverera okondwa.

³² Koma Paulo asanavomereze chomuchitikira ichi . . . Podziwa kuti Mngelo wa Ambuye anali Lawi la Moto, yemwe anali Khristu . . . Chabwino, Iye anali Mngelo wa Pangano, yemwe anali Khristu. Mose anaganiza bwino, moti, anasankha maka kuti amve kuwawa zosautsa ndi anthu a Khristu, ndi kuti azitsozedwa ndi Khristu, kuposa chuma chonse cha Igupto. Iye ankamutsatira Khristu, yemwe anali mu mawonekedwe a Lawi la Moto.

³³ Ndiye Khristu anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu,” pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, “Ine ndikubwereranso kwa Mulungu.” Itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, chiukitsiro, thupi laulemerero akukhala pa dzanja lamanja la Ufumu, kuti azikhalira pakati; Paulo anamuwona Iye ngati Lawi la Moto, kachiwiri: Kuwala komwe kunathimitsa maso ake, pafupifupi; kunamukantha iye khungu.

³⁴ Petro anamuwona Iye atabwera mu ndende ngati Kuwala, ndi kutsegula zitseko patsogolo pake pamene iye anali kutuluka. Ife tikupeza kuti Iye anali Alfa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza.

³⁵ Ndipo apa Iye ali ndi ife, lero, akuchita zinthu zomwe zomwezo zimene Iye ankazichita apo, akudzipanga Iyeyekha kuwonekeranso kwa ife, kuzisonyeza izo kwa dziko lasayansi.

³⁶ O, mu ora lalikulu ili la mdima ndi chisokonezo pa dziko lapansi, ife tikuyenera kukhala anthu okondwetsetsa mu dziko lonse, kuti tizisangalala, podziwa. Nthawi zonse, pamene anthu amwera zigwirizano, ndi mitundu yonse ya timalingaliro ndi zinthu mu dziko, ndipo komabe, lero, Mulungu weniweni, wamoyo, mwa Mawu Ake ndi mwa umboni Wake wooneka, akutisonyeza ife kuti Iye ali pano limodzi nafe, akugwira ntchito, kusuntha, kukhala moyo, kumachita chimodzimodzi basi monga Iye nthawizonse ankachitira. Anthu amwayi omwe ife tiri, pokhala nazo izi! Ife tiyenera ku . . . Baibulo linanena, ndiye, mu mutu wa 2, “Ife tizigwiritse molimba zinthu izi. Chifukwa,

ife tidzathawa bwanji ngati ife tichinyalanyaza chipulumutso chachikulu choterochi?”

³⁷ Tsopano, ife tinabwera apo nkudzapeza kuti, Paulo asanavomereze chomuchitikira icho. . . Tsopano, ife tikuboooleza. Tsopano, ziribe kanthu mtundu wa chokuchitikirani chomwe inu munayamba mwakhalapo nacho, mpingo, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Ziribe kanthu momwe izo zikuwoneka zabwino, momwe izo zikuwoneka zenizeni, izo poyamba ziyenera kuti ziziyesedwa ndi Baibulo. Nthawizonse pa Mawu! Musati konse muzisiya Izo, kwa mtundu uliwonse wa chokuchitikirani.

³⁸ Ndipo Paulo, asanavomereze izo, iye anapita mpaka mu Arabia, ndipo uko anakakhalako zaka zitatu, akuyesa chomuchitikira ichi ndi Mawu. Ndipo pamene iye anabwererako, iye anali wotsimikiza. Palibe chimene chikanamusokoneza iye, pakuti iye anali wolimba pa Mawu, wosasunthika. Ndipo apa ndi pamene iye akupotoloka tsopano kuti awasonyeze kwa Ahebri awa, zinthu zazikulu izo zomwe zinayankhulidwa, za Chipangano Chakale, zinawonetseredwa mwa Yesu Khristu. Ulemerero wakewo!

³⁹ Tsopano, Loweruka lapitali, kapena Lachitatu lapitali, M’bale Neville mkati muno, mu mutu wa 5, anagunda malo ena apamwamba kwambiri, chifukwa iwo ndi mutu wodabwitsa. Ndipo ife tinamupeza iye akuchita ndi mutu wa 4, Lamlungu lapitali, pa *Sabata*, kusunga kwa Sabata. Kodi inu mukutsimikiza, mmawa uno, inu mukudziwa chomwe kusunga kwa Sabata kuli? Ngati inu mukutero, nenani, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

⁴⁰ *Sabata* ndi “Mpumulo” womwe ife timalowamo, osati mwa tsiku, osati mwa lamulo, koma pakulowa mwa Khristu yemwe ali Sabata lathu. Iye ndiye Sabata lathu. Ife tinaziyendetsa izo konse kudutsa mu Chipangano Chakale, ndipo tinasonyeza kuti nthawi ikanadzabwera pamene Mawu akanati adzabwere “mzere pa mzere, langizo pa langizo.” Ndipo Iye anatimikizira kuti ife tinalowa Mpumulo Wake pa Tsiku la Pentekoste, “Pakuti ichi chikanawapangitsa olema kuti apumule, athe.”

⁴¹ Ife tikupeza, kuti, “Mulungu anaikapo tsiku mwa Davide, cha pa tsiku lachisanu ndi chiwiri.” Ndipo, “Mulungu anapuma la chisanu ndi chiwiri.” Anapereka izo kwa—ana a Israeli mu chipululu. “Ndipo kachiwiri, Iye anaikapo tsiku.” Kodi linali tsiku lanji ilo? Tsiku linalake mu sabata? “Tsikulo pamene inu mumva Liwu Lake, musaumitse mtima wanu.” Ndilo tsiku lomwe Iye akulowa umo, kuti akupatseni inu mtendere Wamuyaya, Sabata Lamuyaya.

⁴² Inu simumapita ku tchalitchi Lamlungu, kuti mukhale wachipembedzo, ndiye. Pamene inu mubadwa mwa Mzimu wa Mulungu, inu mumalowa mu Mpumulo kwanthawizonse,

sipamakhalanso kusunga-sabata. Inu muli *mu* Sabata, mopitirira, kwanthawizonse, ndi kwa Muyaya. “Ntchito zanu zachidziko zatha,” limatero Baibulo, “ndipo inu mwalowa mu mtendere uwu wodala.”

⁴³ Mitu yoyamba isanu iyi ikuika mwapamalo Yesu ngati Wansembe Wamkulu. “Mulungu mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyanasiyana ankayankhula kwa makolo kudzera mwa aneneri, koma mu tsiku lotsiriza ili kudzera mwa Mwana Wake, Yesu,” Mutu wa 1, ndime ya 1.

⁴⁴ Ndiye kupitirira mmusi mpaka kothera kwa mutu wa 5, ife tikumupeza Iye akuimiridwa ngati “Melkizedeki, yemwe analibe chiyambi cha masiku, analibe mathero a moyo, koma mopitirira Wansembe kwanthawizonse.” Taganizani za izo. Munthu wamkulu uyu anali ndani? Ife tizipeza izo, mu pafupi mitu ina iwiri yoonjezera. Moyo wonse wa Iye, ife tikuti tiuphunzire. “Munthu wamkulu uyu yemwe anakomana naye Abrahamu, yemwe anali wopanda bambo aliyense, anali wopanda mayi aliyense. Iye analibe nthawi iliyonse yomwe Iye anayamba konse moyo, kapena Iye sadzakhala konse ndi nthawi yomwe Iye ati adzatsirize moyo. Ndipo Iye anakomana ndi Abrahamu akuchokera kokawapha mfumu.”

⁴⁵ Zindikirani Munthu wamkulu uyu, yense yemwe Iye anali, iye akadali moyo. Iye analibe mathero a moyo. Iye anali Khristu, yemwe anakomana naye. Ife tipita mu kuphunzira kwakuya kwa izo, mu masiku pang’ono.

⁴⁶ Tsopano, ife tikufuna kuti tiyambire cha apa mu mutu wa 5 tsopano, kwa maziko aang’ono chabe ife tisanakhudze wa—wa 6, pakuti icho ndi chopambana china kwenikweni. Penyani mwatcheru. Ife tikuti tiyambire pafupi ndime ya 7 ya mutu uwu. Chabwino, tiyeni tiyambire pa ndime ya 6.

Monga iye ananenanso pa malo ena, Ndiwe wansembe kwa nthawizonse monga mwa dongosolo la Melkizedeki.

Yemwe mu masiku ake a mnofu wake, pamene iye . . . anapereka mapemphero ndi mapembedzero ndi kulira kwakukuru . . . misozi kwa . . . iye anali wokhoza kumpulumutsa iye ku imfa, ndipo anamveka popeza kuti ankaopa;

Ngakhale iye anali Mwana, komabe anaphunzira . . . kumvera mwa zinthu zomwe iye adazimva kuwawa;

⁴⁷ Tsopano apa ndi pamene ine ndikufuna kuti ndifikepo, ndime iyi ya 9. Mvetserani. Ine ndikulingalira M’bale Neville anazikhudza izo, Lachitatu. Ine sindinali pano. Chabwino, mvetserani.

Ndipo pamene anapangidwa wangwiro, iye anakhala wopereka wa chipulumutso chamuyaya kwa iwo onse omumvera iye;

Oitanidwa ndi Mulungu wansembe wamkulu monga mwa dongosolo la Melkizedeki.

Za yemwe ife tiri nazo zinthu zambiri kuti tizinene, . . .

⁴⁸ Ife tizisiyira izo apo pa izo, chifukwa ife tikuti tidzamtutenge Melkizedeki mu usiku ungapo.

⁴⁹ Tsopano ife tikuti tiyambire pa izi, kuphunzira kwathu kwachizolowezi. Ine ndikukhumba . . . Ine ndingowerenga zonse za izi kwa mphindi, ndime ya 11.

Za yemwe ife tiri nazo zinthu zambiri zoti tizinene, . . . zovuta kuziyankhula, powona kuti ndinu okumva moperevera.

Pakuti pamene . . . nthawi inu mukuyenera kukhala aphunzitsi, inu muli nako kusowa koti wina akuphunzitseni inu aponso zomwe ziri mfundo zoyambirira za maneno a Mulungu; ndipo mwakhala onga ngati omwe akusowa mkaka, mmalo mwa chakudya champhamvu.

Pakuti aliyense wogwiritsa ntchito mkaka alibe luso mu mawu a chirungamo: pakuti iye ali khanda.

O, ine ndikuyembekeza kuti Mzimu Woyera watengera izo pansi pomwe mwa inu tsopano.

Pakuti iye y—yemwe agwiritsa ntchito mkaka alibe luso mu mawu a chirungamo: pakuti iye ali khanda.

⁵⁰ Inu mukamupatsa khanda chakudya cholimba, inu mumupha iye. Ndicho chifukwa anthu ambiri amati, “A, i—ine sindikukhulupirira izo,” ndi kuchokapo. Akadali makanda! Iwo sangakhoze kumvetsa basi. Iwo sangakhoze basi kuchigwira Choonadi chimenecho. I—Icho chimawapha iwo. Zinthu zazikulu, zamphamvu zomwe mpingo ukuyenera kumazidziwa lero, koma inu simungakhoze kuziphunzitsa Izo. I—i—i—i—iwo amaphunthwa pa Izo. Iwo samadziwa choti achite nazo Izo.

⁵¹ Paulo, akuyankhula kwa gulu la Ahebri ili . . . Komabe, iye akuyankhula kwa masikolala tsopano, masikolala, ophunzira bwino. Ife tipeza izo, mu zochepa—mphindi zochepa, ophunzira kwambiri. Koma Chinsinsi chakuya chauzimu, mpingo ukadali wakhungu kwa Icho. Iye anati, “Pamene inu mukuyenera kuti muziwaphunzitsa ena, inu mukadali makanda.”

⁵² O, ine ndikudziwa alipo ambiri atauke ndi kutuluka nkumati, “O, ine sindikusowa kuti ndizipita ku tchalitchi panonso. Mulungu alemekezeke, Mzimu Woyera wabwera, Iye ndi mphunzitsi.” Pamene inu mupeza ganizo limenelo, inu muli basi kulakwitsa. Pakuti nchifukwa chiani Mzimu Woyera unaika

aphunzitsi mu mpingo, ngati Iye ali woti akhala mphunzitsi? Mukuona? Poyamba pali atumwi, aneneri, aphunzitsi, alaliki, ndi abusa. Mzimu Woyera unaika aphunzitsi mu mpingo, chotero Iye azikhoza kuphunzitsa kupyolera mwa mphunzitsi ameneyo. Ndipo ngati i—izo siziri molingana ndi Mawu, Mulungu sazitsimikizira izo, ndiye si mtundu wolondola wa kuphunzitsa. Izo ziyenera kuti zizifanana ndi Baibulo lonse, ndi kukhala zamoyo basi lero monga Izo zinali apo. Apo pali chinthu chenicheni chiri kuwonetseredwa.

⁵³ Tsopano zindikirani.

Koma chakudya cholimba ndi cha kwa iwo omwe ali . . . akulu msinkhu, ngakhale iwo amene mwa zifukwa amagwiritsa ntchito . . . agwiritsa ntchito zokhudzira zawo kuti azindikire chabwino ndi choipa.

Kudziwa chomwe chiri chabwino ndi chomwe chiri cholakwika, mwa kuzindikira za mumtima.

⁵⁴ Tsopano zindikirani, tikuyamba tsopano pa phunziro lathu. Maziko aakulu awa tsopano, tiyeni tipite ku ndime ya 1.

Chotero posiya zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, . . .

Kodi iye akuti chiani? Mitu yonse yoyamba isanu iyi yakhala itaikidwa pa Khristu, kuti tisonyeze yemwe Iye ali. Tsopano ife tikusiya zoyambirira izo za ziphunzitso za Khristu.

⁵⁵ Kodi ife tamupeza Iye kuti ndi chiani? Ife tamupeza Iye kuti ndi Yehova Mulungu wamkulu atawonetseredwa mu thupi. Ife tinamupeza Iye k—kuti sanali mneneri, koma chidzalo cha Umulungu mu thupi. Iye anali Yehova atapangidwa thupi. Ndipo thupilo, Yesu, linangokhala kachisi wa Iye. Mulungu akukhala mwa munthu. Mulungu kukhala akuyanjanitsidwa kwa anthu, kudzera mwa munthu, mwa kubadwa mwa namwali kwa Mwana Wake yemwe. Ndipo Yehova, Mzimu, ankakhala mwa Iye.

⁵⁶ Tsopano, ndi angati akukumbukira kuphunzitsa kwa Umulungu, momwe ife tinapitira mmbuyo ndi kukamupeza Mulungu ngati utawaleza wawukulu uli ndi mtundu wonse wa Mzimu, momwe Iwo unaliri? Ndiyeno Logos inapita kuchokera kwa Mulungu, yomwe inadzakhala fiofane, ndi yomwe inali mwa mawonekedwe a munthu. Ndipo Mose anaiwona Iyo ikudutsa apo, mkati mwa thanthwe. Ndipo kenako fiofane imeneyo inapangidwa mwamtheradi thupi laumunthu, Khristu.

Ndipo momwe ife tinapezera kuti ife, kupyolera mu chisomo Chake, tiri nawo Moyo Wamuyaya. Tsopano, mawu okuti *kwanthawizonse* ndiwo “kwa mtunda; kwa danga la nthawi.” Izo zinanenedwa, mu Baibulo, “Kwanthawi *ndi* nthawi,” cholumikizira. Koma *kwanthawizonse* amatanthauza kokha “nthawi.” Koma Muyaya umatanthauza *kwanthawizonse*. Ndipo chirichonse chokha chomwe chinali ndi chiyambi chiri ndi

mapeto, koma zinthu zomwe zinalibe chiyambi ziribe mapeto. Koteru Mulungu analibe chiyambi ndipo Iye alibe mapeto.

⁵⁷ Ndipo choncho, chotero, Melkizedeki, Wansembe wamkulu, wonga munthu, Iye analibe chiyambi ndipo Iye alibe mapeto. Ndipo pamene ife, kudzera mu fiofane imeneyo, yomwe, ife tinapangidwa mwa chifanizo cha Mulungu dziko lisanapangidwe nkomwe; pamene fiofane imeneyo inakhala itapangidwa thupi ndipo inakhala pakati pathu, ndiye, kudzera mu imfa Yake, ife eniathu talandira Mzimu Wake ndipo ife tiribe mapeto; Moyo Wamuyaya; osati Angelo, koma amuna ndi akazi. O, i... Mwanjirayina, ngati ine ndikanangokhoza kuzitenga izo mwanjira yakuti o—omvetsera anga akanati azimvetse izo! Inu simudzakhala konse Mngelo. Mulungu anapanga Angelo, koma Mulungu anamupanga munthu. Ndipo chimene Mulungu amachita ndi chochokera kwa Mulungu, chomwe chiri Chamuyaya momwe Mulungu aliri. Ndipo munthu ali basi Wamuyaya monga Mlengi wake, chifukwa iye anapangidwa kuchokera ku Umuyaya.

⁵⁸ Koma tchimo liri nawo mapeto, kuzunzika kuli nawo mapeto. Chotero, sikungakhoze kukhala kuli gehena Wamuyaya. Alipo gehena, moto ndi miyala ya surfule, ife tikudziwa zimenezo, koma kulibe gehena Wamuyaya. Kuli mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya ndipo umenewo ndi wa Mulungu. Ngati inu muli oti mukazunzike kwanthawizonse, inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Gehena ali ndi mathero, izo zikhoza kukhala zaka mabilioni, koma iye potsiriza adzafika ku mathero.

⁵⁹ Baibulo silimanena, paliponse, kuti iwo anazunzidwa Kwamuyaya, linati, “Kwanthawi za nthawi.” Yona ankaganiza kuti iye anali mu mimba ya chinsomba “kwanthawizonse,” nayenso. *Kwanthawizonse* ali ndi mtunda kapena muyezo wa nthawi. Koma *Muyaya* ndi wopitirira, iwo ulibe chiyambi kapena mathero. Iwo uli ngati mphete, nkombero. Ndipo pamene nthawi yathu ikusuntha, ife tikungozungulira pa zochititsa zazikulu za Mulungu.

⁶⁰ Chochititsa cha Mulungu chinali kuti adzapange munthu mu chifanizo Chake, kuti aziyanjana naye Iye. Ndipo Iye anamupanga iye chinthu chogwirika. Tsopano, tchimo linatibweretsa ife mu malo a—a—a chivundi, koma izo sizimaimitsa konse dongosolo la Mulungu. Ndipo, mzanga wochima, lero, ngati iwe sunabadwe kachiwiri mwa Mzimu wa Mulungu, iwe uli nawo mathero kwinakwake. Ndipo mathero ako ndi chisokonezeko, mu kuwonongeka, ndi kuzunzika ndi chisoni. Koma kwa inu omwe mwakhulupirira pa Ambuye Yesu, ndipo mwamulandira yemweyo ngati Mpulumutsi wanu wanu, ziri Zamuyaya basi monga Mulungu aliri Wamuyaya. Inu mulibe mapeto, “Ine ndimapereka kwa iwo *Zoe* Wamuyaya, Moyo wa Mulungu womwe, ndipo iwo sadzawonongeka konse kapena

kubwera mu chiweruzo, koma adutsa kuchokera ku imfa apita ku Moyo.” Ndi chomwe Iye anali. Ndi chomwe Iye anadzera.

⁶¹ Tsopano, Yesu, mu kudza Kwake, kwa unsembe Wake, sanangobwera basi pa cholinga cha chisoni. Anthu ambiri amaphunzitsa izo monga choncho, kuti Iye anabwera, nati, “Chabwino, mwinamwake ngati ndivutika, ine ndikhala c—c—chionekedwe chomvetsa chisoni ndipo anthu ndithudi azibwera kwa Ine.” Uko ndi kulakwitsa. Palibe Lemba la zimenezo.

Pakuti, munthu aliyense yemwe ati adzapulumutsidwe konse, Mulungu anawadziwa iwo dziko lisanawumbidwe konse. Baibulo linanena chomwecho. “Mulungu sakulolera kuti aliyense awonongeke.” Iye akufuna kuti onse abwere ku kulapa. Koma, pokhala Mulungu, mwa kudziwiratu Iye anazidziwa izo.

⁶² Yang’anani mu Aroma, mutu wa 8. Paulo anali kugwiritsa apo, akunena za kusankha kwa Mulungu, kuti, “Esau ndi Yakobo mwana aliyenseyo asanabadwe, kapena chirichonse, Mulungu ananena kuti Iye ankawadziwa iwo ndipo Iye ankamuda Esau ndipo ankamukonda Yakobo,” mwana aliyenseyo a—asanakhale nawo mwayi woti afotokoze kuyamikira kwawo, pakuti Iye anali Mulungu. Iye amadziwa . . . Iye ndi wopandamalire. Ngati Iye ali wopandamalire, Iye ankaudziwa utitili uliwonse, ntchentche iliyonse, mavu aliwonse, chirichonse chomwe chikanati chidzakhale pa dziko lapansi. Iye ankachidziwa icho. Iye ndi wopandamalire, Wamuyaya, wachisavundi, Mulungu wodala, wamphamvuzonse, wopezeka paliponse, wodziwa zonse. Palibe chinthu chimene Iye samachidziwa. Ndicho chifukwa Iye akhoza kunena chomwe mapeto ati adzakhale. Iye ankadziwa mapeto kuchokera ku chiyambi.

⁶³ Chomwe chiri chauneneri ndicho chidziwitso Chake chabe. Iye ndi woimira mlandu wamkulu. Iye, Iye ali . . . Iyeyo ndi woweruza. Ndipo Iye amangoyankhula kwa—woyimira mlandu zina za nzeru Zake. Ndipo icho nchomwe uneneri uli, kuti akhoza kuneneratu izo, chifukwa Iye amadziwa chomwe chiti chidzakhalepo. Tsopano, ndi ameneyo Mulungu yemwe ife timamutumikira. Osati mulungu wa mbiriyakale, osati monga Achibuddha ndi Achimuhamadi, ndi zina zotero. Koma, Mulungu yemwe ali wopezeka paliponse, pakali pano muno, mmawa uno, mu kachisi uyu pakali pano; Yehova Wamkulu, INE NDINE, Yemwe anadziwumba Iyeyekha mwa kudzichepetsa, kuti atenge mawonekedwe a thupi lodzaza machimo. Ndi Uyu apa. Ndi yemwe anakuwombolani inu. Sipangakhoze kukhala winanso, kulikonse, palibe nthawi ingakhoze kuchita izo.

⁶⁴ Mulungu analibe anthu atatu kumwamba uko, ndipo Iye nkumutuma mmodzi wa iwo, Mwana Wake. Uyo anali Mulungu, Mwiniwake, atabwera mu mawonekedwe a Mwana. Mwana ali nacho chiyambi, ndipo Mwana anali nacho chiyambi. Izo, ena a inu anthu okonedwa Achikatolika, ine ndiri

nalo bukhu lanu, *Zoona Za Chikhulupiro Chathu*, limati, “Umwana Wamuyaya wa Mulungu.” Inu mungalongosole bwanji mawu amenewo? Inu mungawapange bwanji iwo kukhala ndi zomveka? Ungakhoze bwanji iwo kukhala Wamuyaya? Limenelo si Baibulo. Limenelo ndi bukhu lanu, “umwana Wamuyaya.” Iwo sali... Mawu amenewo si olondola. Pakuti, chirichonse chomwe chiri mwana chinali ndi chiyambi, ndipo Muyaya ulibe chiyambi, chotero si umwana Wamuyaya. Khristu anakhala thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Iye anali ndi chiyambi. Panalibe umwana Wamuyaya. Ndi Umulungu Wamuyaya, osati umwana. Tsopano, Iye anabwera kuti adzatiwombole ife, ndipo Iye anatiwomboladi ife.

⁶⁵ Tsopano, Paulo, pofika apa, chimene ine ndikutsimikiza kuti kupyolera mmaphunzitso ammbuyowa inu mwamvetsa izo. Ife tidzadutsa mu izo kachiwiri, nthawiyina, Ambuye akalola, mwa ndime ndi ndime basi, tsopano.

Chotero pokhala . . . posiyana nazo z—zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro; . . .

⁶⁶ Izo zimawaphunthwitsa iwo. Sichoncho izo? Tiyeni ife tichite chiani?

. . . tiyeni tipitirire mpaka ku ungwiro; osati kuikanso maziko . . .

⁶⁷ Penyani izi. Tiyeni titenge mawu awa “ungwiro.” Kodi inu mukudziwa kuti ilipo njira imodzi yokha yomwe inu muti mudzakaima mu Kukhalapo kwa Mulungu? Ndiyo, ungwiro. Mulungu sangakhoze kulekerera zinthu zosayera.

⁶⁸ Ndipo inu azamalamulo: inu mungathe bwanji kudzipangitsa nokha angwiro, pamene inu mulibe kanthu kamodzi koti mudzipangitse nako nokha angwiro? Inu munabadwa mu tchimo. Kuyembekezeredwa kwanu komwe kunali mu tchimo. Chikhumbo chomwe choti inu mukhale kuno ndi tchimo. “Munabadwa mu tchimo, munawumbidwa mu kusaeruzika, munabwera mu dziko nkumayankhula bodza.” Tsopano kodi inu mudzakaima pati?

⁶⁹ Uli kuti, wochimwa, y—yemwe unati, “Ine ndisiya kusuta. Ine ndipita Kumwamba?” Kodi uli kuti, wofunda, wansana wandere, wotchedwa Mkristu, yemwe umayenda yenda kuno ndi nkhope yaitali ndi kumanena, kuti, “Chabwino, ine ndine wa mu mpingo?” Iwe wochimwa. Ndiko kulondola. Kupatula ngati iwe utabadwa wa Mzimu wa Mulungu, iwe wataika. Ndi zoona.

⁷⁰ Iwe udzapita bwanji Kumwamba? Iwe ukuti, “Ine sindinayambe ndanamapo mu moyo wanga. O, wokonedwa wamng’ono. I—izo anali Mngelo yekha, pa kuyamba pomwe.” Ilo ndi bodza. Ine sindikusamala momwe inu muliri wabwino; ndinu ochimwa. Ndipo inu mulibe kanthu kamodzi; palibe wansembe, palibe bishopu, palibe kardinolo, palibe papa, ngakhale kanthu

kalikonse kangakhoze kukupulumutsani inu, chifukwa iye ali mu bwato lomwelo limene inu mulimo. Ife tikufika kwa izo mu maminiti pang'ono. Mu mawumbidwe omwewo omwe iye anali. Papa waku Roma anabadwa mu tchimo, anawumbidwa mu kusaweruzika, anabwera mu dziko akunena bodza, anabadwa mwa chikhumbo chakugonana cha mwamuna ndi mkazi. Inu mukachitenga pati chirungamo kuchokera mu zimenezo?

⁷¹ “Chabwino, bambo ake ndi amake anabadwa mwa njira yomweyo, ndipo iwo anabadwa mwa njira yomweyo, ndipo agogo ake aakazi ndi agogo amuna ndi mpaka mmbuyo.” Ndi tchimo, pa kuyamba pomwe!

⁷² Chotero nndani angakhoze kunena kuti *uyu* ndi woyera ndipo *uyo* ndi woyera? Pali chinthu chimodzi chokha choyera, ndicho Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo, Yemwe anapangidwa Wangwiro. Ndipo chofunikira chathu nchakuti tikhale angwiro. Tsopano, kodi ife tikhala motani izo? Yeserani izo, inueni. Ine ndikanadana nazo kuyesera kuti ndikafike Kumwamba pa zondiyenereza za kuti, “Ine ndinabadwa maminiti asanu apitawo, ndipo ndikuchoka mu dziko pakali pano.” Ine ndikanati ndikhale wotaika. Ngati ine sindinayambe ndakhalapo ndi lingaliro loipa mu moyo wanga, ngati ine sindinayambe ndayankhulapo mawu oipa mu moyo wanga, ngati ine sindinayambe ndayang'anapo pa chirichonse choipa, sindinaganizepo chirichonse choipa, kapena palibe kena, ndine basi wa mgululo ndi wakuda monga makoma onyansa aku gehena. Ndine wochimwa.

⁷³ Ine ndikhoza kubwera kudutsa mmoyo ndi kukhala wotsekeredwa mu chipinda, ndi monga ena a alongo Achikamerlo kapena chinachake, ndi kusamaliwona konse dziko, kukhala mmenemo ndi kumapemphera, moyo wanga wonse, kumachita zabwino, kubadwa ndiri ndi mamilioni ambiri ndi kumapereka kwa osauka chirichonse chomwe ine ndiri nacho, ndipo ndine wochimwa apabe ndipo ndidzapita ku gehena. Inde, bwana.

⁷⁴ Ine ndikhoza kujowina mpingo wa Chilutera, Baptisti, Pentekoste, Presbateria, pamene ine ndiri pa gulu la makanda, ndi kukhala wokhulupirika kwa mpingo umenewo mpaka zaka zana, ndipo moyo wanga nkutengedwa, ndipo nkusakhalapo munthu yemwe akanaloza chala chake pa ine nkuti “Iye sanayambe wakhalapo nalo nkomwe ngakhale lingaliro loipa,” ine ndidzapita ku gehena motsimikiza basi monga ine ndaimiramu.

⁷⁵ Ndine wochimwa. Uko nkulondola. Ine ndiribe kalikonse. Palibe njira, konse, ine ndingakhoze kupezera uliwonse—mtengo uliwonse woti ulipiridwe. Mulungu anafuna imfa. Ndipo ngati ine ndingapereke moyo wanga womwe, ngati ine ndingapereke moyo wanga, ndiye ine ndingathe bwanji kulapa? Chifukwa,

inu. . . Ngongoleyo iyenera kuti iperekedwe, choyamba. Ndipo Mulungu anali Mmodzi yekha yemwe akanakhoza kuika moyo Wake pansi ndi kuwutengaponso Iwo kachiwiri. Chotero Iye akanakhoza kukhala tchimo, ndi kuika Moyo Wake pansi ndi kuwutengaponso Iwo, ndi kuchitcha icho “chilungamo,” ndipo ngongole yaperekedwa. Ndi inu apo.

⁷⁶ Tsopano tiyeni titembenuzire ku Mateyu, cha pa mutu wa 8, ine ndikukhulupirira apo pali, mutu wa 7 kapena wa 8. Ife tiwona zomwe Yesu akunena pamenepa. Chabwino. Ndi Mateyu, mutu wa 5. Ndipo. . . Yesu, kulalikira, akulalikira mu chiphunzitso cha paphiri, ndime ya 47.

Ndipo ngati inu muwalonjera abale anu okha, nchiani chomwe inu mukuchita kuposa ena? Kodi satero ngakhale amisonkho. . . ? (Penyani.)

Koma khalani inu chotero angwiro, . . . (Chiani?)

Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu omwe ali kumwamba ali angwiro.

Ilo linali lamulo la Yesu, “Khalani inu chomwecho.”

⁷⁷ Iwo amati, “Palibe wina angakhale wangwiro, Baibulo linati, ‘Palibe wina ali wangwiro.’ Ndi uko kutsutsana kwanu.” Si choncho? Chabwino.

⁷⁸ Inu simungakhoze kukhala angwiro mwa inueni. Ngati inu mukudalira mu zomwe inu mwazichita, inu mwataika. “Chotero khalani inu angwiro, ngakhale wangwiro monga Mulungu aliri wangwiro.” Tsopano:

Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu. . . kumwamba ali angwiro.

⁷⁹ “Chotero. . .” Tsopano mutu wa 5, mutu wa 6 wa Ahebri.

Chotero posiyana nazo zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro; . . .

⁸⁰ Tsopano, inu, Branham Tabernacle. O, ine ndikudziwa, “Ife tiri nawo machiritso.” Izo nzodabwitsa. “Ife tiri nawo masomphenya.” O, ndi—ndizo zabwino. Ndipo inu mumakhala nawo maloto auzimu, ndipo nthawizina iwo samakhala maloto auzimu. N—ndipo nthawizina inu. . . “Ife, ife timayesera kuwathandiza osawuka. Ife timachita zomwe ife tingathe.” O, izo zonse ndi zabwino, koma sindizo zomwe ife tikuzikamba tsopano. Ife tikulowa mu gawo lina.

. . . posiyana nacho. . . chiphunzitso. . .

⁸¹ “O, inde, ife tiri nacho chiphunzitso cha Khristu. Ife timakhulupirira kuti Iye anali Mwana wa Mulungu, ndi wobadwa kwa namwali. Ife timakhulupirira zimenezo, ndi zinthu zonse izi.” Izo ndi zodabwitsa basi.

⁸² Koma, “Kuzisiya izo, tiyeni tipitebe mpaka ku ungwiro.” O, mai! Ndikukhumba ine ndikanakhala nalo liwu la mngelo

wamkulu tsopano, kuti ndizibweretse izi pa malo pomwe inu mukanakhoza kuziwona izo. Tsopano iye akuti, “Kusiya chiphunzitso chonse cha Khristu,” a—fioloje onse, ndi fioloje yonse yomwe ife tikuidziwa, zonse za Umulungu wa Khristu, momwe Iye anali Mulungu atapangidwa thupi, zinthu zina zonse izi.

⁸³ Paulo akupitirira kufotokoza izo zonse apa, mu maminiti pang’ono okha. Tiyeni tingowerenga izo, pang’ono pokha, ife tisanafike kwa izo.

... kuikanso maziko a kulapa kuchokera ku ntchito zakufa...

Tsopano, ife timakhulupirira zimenezo.

... ndi chikhulupiriro cha kwa Mulungu,

Ife timakhulupirira zimenezo.

Ndi za chiphunzitso cha maubatizo,...

Basi momwe inu muyenera kumabatizidwira, ife timakhulupirira zimenezo.

... ndi za kusanjika kwa manja,

Ife timakhulupirira mu kusanjika kwa manja. Sichoncho ife? Mukuona, zonse izo, zedi.

... ndi za chiukitsiro cha akufa,...

⁸⁴ Ife timakhulupirira zimenezo. Tsopano penyani. Inu mukuona apa, “Chiweruzo,” chikugwiritsidwa ntchito, “Chamuyaya.” Ichu ndi chanthawizonse. Pamene chiweruzo chiyankhulidwa ndi Mulungu, ndi chanthawizonse. Ndiye, sikungadzakhale chiyanjantitso china chiweruzo chitaperekedwa kale. Tsopano inu mukhoza kumvetisa chifukwa chimene Mulungu anachita kutenga Ake Omwe—Ake Omwe, monga ife tingawatchulire iwo, mankhwala Ake Omwe. Pamene Iye anamuweruza munthu pa kuchimwa, njira yokha yomwe Iye akanakhoza kuyanjanitsira, inali yodzatzenga malo a munthu Iyemwini. Ndiyo njira yokha yomwe iye akanakhoza kuyanjanitsidwira, kapena akanati ayanjanitsire ife, inali kutenga malo athu ndi kukhala wochimwa. Mulungu, Yehova, anakhala wochimwa, ndipo Iye anapereka moyo Wake.

⁸⁵ Tsopano, inu mukanakhoza kupereka moyo wanu, monga wochimwa, kuti mufere cholingacho. Paulo anati, “Ngakhale ine ndingapereke thupi langa alitenthe ngati nsembe, ine sindiri kanthu apobe,” chifukwa izo sizigwira ntchito. Mukuona, pamene inu mufa, inu mwapita. Inu mukafa ngati wochimwa, inu mwataika.

⁸⁶ “Koma Mulungu anabwera pansu mu mnofu, ndipo analiweruza tchimo mu mnofu, pokhala anapangidwa mnofu machimo.” Chifukwa, Iye anali Mulungu Wamuyaya,

ndipo analidzutsa thupi Lake lomwe apo, koteru Iye ndi wolungamitsa.

⁸⁷ Tsopano, zinthu zonse izi, “Tiyeni tipitirire mpaka ku ungwiro,” anatero Paulo. Tsopano chiani?

...za chiweruzo chamuyaya.

...izi ife tidzachita,... Mulungu akalola. (Ndime ya 3.)

⁸⁸ Tsopano, “Pitirirani mpaka ku ungwiro.” Yesu anati, “Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu Kumwamba ali angwiro.”

Ndipo ife tiri, aliyense, wotsutsidwa. Ziribe kanthu zomwe tinayamba tachitapo, ndife otsutsidwa. Ife tinabadwa, otsutsidwa. Amayi anu ndi abambo anu anabadwa, otsutsidwa. Inu, makolo anu onse, anabadwa mu tchimo, anawumbidwa mu kusaweruzika. Koteru kodi inu muzipeza bwanji izo konse? Inu mukhala bwanji angwiro konse? Ngati inu simunayambe mwachitapo chinthu, simunabepo, simunanamepo, simunayambe mwachitapo chirichonse mu moyo, ndinu otsutsidwabe. Inu munatsutsidwa musanapume konse mpweya wanu woyamba. Inu munatsutsidwa. Ndiko kulondola. Ndipo inu munaweruzidwa ndi Mulungu musanapume mpweya wanu woyamba. Pakuti inu munaweruzidwa, ndi chikhumbo cha kugonana cha abambo anu ndi amanu omwe, kupyolera mu kuchita kwawo, anakubweretsani inu kuno padziko lapansi. Ndipo Mulungu anazitsutsa izo, pachiyambi pomwe. Ndinu otsutsidwa, pakuyamba pomwe. Koteru ndi pamene inu... Ndipo munthu wina aliyense pa dziko lapansi anatsutsidwa limodzi ndi inu. Tsopano nkuti komwe inu muti mukawutenge ungwiro?

⁸⁹ Penyani. Tiyeni titembenuzire kwa mphindi yokha ku Ahebri, mutu wa 10. Mvetserani mwacheru. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge pang’ono pokha kuchokera ku mutu wa 9, poyamba, ndime ya 11

Koma Khristu pokhala wansembe wamkulu wa zinthu zabwino zinali kudza, mwa kachisi wamkulu ndi wangwiro kwambiri, kachisi wake yemwe, thupi lake,...

⁹⁰ Mukuona, kachisi wakale, inu mukuzindikira, kachisi wakale anali ndi chotchinga mmenemo, chomwe chinkabisa likasa komwe Mulungu ankakhalako. Ndi angati akudziwa zimenezo? Zedi. Chabwino, kachisi wakale uja wopangidwa ndi anthu kuno, zotchinga zochokera ku zikopa za mbuzi zolochedwa, ndi zina zotero, zinapangidwa kachisi kuti azibisamo Kukhalapo kwa Mulungu. Ndi angati akudziwa kuti munthu mmodzi yekha ankakhoza kupita mmenemo kamodzi pa chaka? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndithudi. Ameneyo anali Aroni, ankalowamo kamodzi pa

chaka. Ndipo iye ankayenera kuti akhale atadzozedwa. N—ndi, o, chofunikira! Ndipo iye ankayenera kuti azikhala ndi moto mu dzanja lake; ndipo ngati iye akanapita wopanda zimenezo, iye ankafa mwamsanga pamene iye ankasunthira chotchinga icho mmbuyo. Iye ankakhoza kugwa nkufa. Iye ankayenera kuti apite mmenemo ndi kukayatsa nyali izi, ndi kuwuwaza mpando wa chifundo umene unkafulira apo, magazi a imfa, cholowezammalo, mpaka Khristu anali woti abwere kudzakwaniritsa izo.

⁹¹ Tsopano, koma, Mulungu ndiye anakhala mu mtundu wina wa kachisi. Ndipo kachisi ameneyo anali ndani? Yesu. Ndipo Mulungu anali mkati mwa Yesu, ndipo Iye anabisidwa, koma Iye anali akuliyanjantsa dziko kwa Iyemwini, mwa kulongosolera Kwake. Khristu anamuulula Mulungu. Iye anati, “Si Ine yemwe ndikuchita ntchitozi. Ndi Atate Anga omwe akukhala mkati Mwangwa. Ine sindichita kanthu mwa Inemwini koma zomwe Ine ndiwawona Atate akuchita. Atate mkati Mwangwa, akundisonyeza Ine masomphenya awa, ndiyeno ine ndikumapita ndi kumachita basi zomwe Atate akundiiza Ine kuti ndizichita.” Inu mukuzimva izo? Mulungu anali mkati mwa thupi laumunthu, osati kuseri kwa zikopa za mbuzi zolochedwa, koma anali wa moyo, akuyenda. Mulungu anali ndi manja; Mulungu anali ndi mapazi; Mulungu anali ndi lirime; Mulungu anali ndi maso; ndipo izo zinali Khristu. Apo Iye anali.

⁹² Tsopano, Iye anachokapo, ndipo Mzimuwo unabwera mmenemo, kuti kupyolera mu imfa Yake Iye akakhoze kupangitsa Mpingo kukhala wangwiro ndi kuwubweretsa Mpingo pomvera. Ndiyeno Mzimu womwewo umene unali mwa Khristu uli mu Mpingo, ukuchita zinthu zomwezo zimene Khristu ankazichita. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silimandiwona Ine kenanso; komabe inu muzindiwona Ine, pakuti Ine ndizikhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka ku mathero a dziko.”

⁹³ Tsopano mvetserani kwa izi.

Koma Khristu kukhala wansembe wamkulu wa zinthu zabwino zakudza, mwa kachisi wamkulu ndi wangwiro kwambiri, osati wopangidwa ndi manja, uko nkunena kuti, osati wa nyumba iyi;

Iye sanali wopangidwa ndi manja. Kodi Iye anabadwa chotani? Kubadwa mwa namwali.

Osatonso mwa magazi a mbuzi ndi a ng’ombe, kuti thupi ili linayamba laperekedwapo nsembe kapena linayeretsedwapo, koma mwa magazi ake omwe . . .

⁹⁴ Inu mukudziwa kuti magazi amachokera kwa chiwalo champhongo. Ndiyeno winawake anati, “O, Yesu anali Myuda.” Iye sanali Myuda. “O, ife tinapululumutsidwa ndi magazi

Achiyuda.” Ayi, ife sitiri. Ngati ife tinapulumsidwa ndi magari Achiyuda, ife tikanali otaika.

Yesu sanali Myuda, ngakhalenso Iye sanali Wamitundu. Iye anali Mulungu: Mulungu Atate, Mzimu, Mmodzi wosawonekayo. “Palibe munthu anamuwonapo Mulungu pa nthawi inayonse, koma wobalidwa yekhayo wa Atate wamufotokoza Iye.” Iye anawonetsera Mulungu, chomwe Mulungu anali.

⁹⁵ Tsopano Mpingo Wake ukuyenera kuti uziwonetsera Mulungu, kuti usonyeze chomwe Mulungu ali. Mukuona?

Kodi ife tikuchita chiani? Tikudzipanga tokha bungwe, ndi, “Ine ndiribe kanthu koti ndizichita ndi *iwo*. Iwo ndi Achimethodisti. Iwo ndi Achipresbateria. Ine sindikufuna kanthu komachita nawo *iwo*. Ndine wa Chibaptisti. Ndine wa Chipentekoste.” Nha! Inu mwataika, ndi mtundu uwo wa chokupangitsani. Kulondola.

⁹⁶ Ndani angadzibwekerere? Ndani anganene chirichonse? Tayang’anani pa chamanyazi chomwe Achipresbateria abweretsa. Tayang’anani pa chamanyazi, Achibaptisti. Tayang’anani pa chamanyazi, Achikatolika. Tayang’anani pa chamanyazi, Achipentekoste, Anazerene, A Pilgrim Holines. Tayang’anani pa iwo onse.

Koma, ine ndikukutsutsani inu kuti muloze dzanja limodzi, mwa chamanyazi, pa Ichu. Eya. Lozani chala chimodzi, pamene Mulungu Wamphamvuzonse anati, “Uyu ndi Mwana wanga wokonedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo. Mvereni inu Iye.” Ndi Uyo apo. Ameneyo ndiye Wangwiroyo.

⁹⁷ Tsopano, tiyeni tiwerenge mopita patsogolo pang’ono apa tsopano.

Ngakhalenso osati mwa magari a mbuzi. . . ang’ombe, koma ndi magari ake omwe iye analowamo kamodzi mu malo oyera, atapindula chiwombolo chamuyaya . . . (Kodi inu mukumvetsa izo?) . . . chiwombolo chamuyaya kwa ife.

⁹⁸ Osati kuti tiwomboledwe lero, ndiyeno, sabata yamawa pamene chitsitsimutso chiti chiyambe, nkudzawomboledwa kachiwiri, ndiyeno, o, ife ntibwerera mmbuyo ndipo nkudzawomboledwa kachiwiri. Inu mumawomboledwa kamodzi, kwanthawizonse. Ndiko kulondola. Sipamakhalanso kuwombola, wombola, wombola. “Chiwombolo Chamuyaya!” “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wa,” tensi yakale, “wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Chifukwa iye wanjenjemera? Chifukwa iye anabatizidwa mwanjira inayake? Chifukwa iye anali ndi magari mu dzanja lake? “Chifukwa iye wakhulupirira pa Mwana wobalidwa yekhayo wa Mulungu.” Ndi momwe ife timalandirira chiwombolo Chamuyaya.

99 Mvetserani tsopano.

Pakuti . . . magazi a ng'ombe ndi a mbuzi, ndi mapulusa a ng'ombe ankakonkhedwa—a . . . ankakonkha chosayeracho, ankayeretsa kuti apangitse ungwiro wa thupilo:

Ndi mochulukwa bwanji momwe magazi a Khristu ati adzatero, yemwe kupyolera mu Mzimu wamuyaya anadzipereka yekha wopanda banga kwa Mulungu, anatsuka chikumbumtima chathu ku ntchito zakufa kuti tizimutumikira Mulungu wamoyo?

100 “Wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Mukusamala chiani pa zomwe dziko likuganiza? Mukusamala chiani pa zomwe oyandikana nanu akuganiza? Chikumbumtima chathu chafa, ndipo ife tasinthidwa ndipo tabadwa kachiwiri mwa Mzimu wa Mulungu, kuti tizimutumikira Mulungu woona ndi wamoyo. Ndi inu apo.

101 Tsopano tigwere ku ndime ya 10 . . . mutu wa 10, kani, kungwoloka tsambalo.

. . . lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zinali nkudza, ndipo osati fanizo lomwe la zinthuzo, silingakhoze ndi nsembe izo zomwe iwo ankazipereka chaka ndi chaka kupitirira kumupanga wobwerakoyo w-a-n-g-w-i-r-o.

U-n-g-w-i-r-o, uli pamenepo, “Ungwiro.”

. . . kusiyana nazo zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro; . . .

Khalani inu chotero angwiro, ngakhale monga Atate anu . . . kumwamba ali angwiro.

102 “Lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zakudza,” malangizo onse ndi maubatizo ndi . . . zinthu zina zonse zomwe iwo anali nazo, “sizikanakhoza kumupanga wopembedzayo kukhala wangwiro.” Ndipo, komabe, Mulungu akufuna “wangwiro.”

103 Inu mukajowina mpingo wa Nazarene, sudzakupangani konse inu kukhala angwiro. Inu mukajowina mpingo wa Baptisti, Chipentekoste, uliwonse womwe uli, iwo sudzakupangani konse inu kukhala angwiro. Inu pokhala munthu wabwino, womvera, sizidzakupangani konse inu kukhala angwiro. Inu simungapindule chinthu chimodzi. Pali chinthu chimodzi cha inu, kuti mupindule. Inu mwataika. Inu mukuti, “Chabwino, ine ndimasunga lamulo. Ine ndasunga sabata. Ine ndimasunga izi, malangizo onse a Mulungu. Ine ndimachita izi.”

104 Paulo anati, “Tiyeni ife tiyike kumbali zinthu zonse izo tsopano.”

105 “Zonsezo ndi zabwino, koma ife tizichita *izi*. Ife tiziwabatiza anthu, ndipo ife tiziika manja pa iwo kwa machiritso awo ndi zina zotero.”

106 Ife tikhoza kuzitenga izo, ndime ndi ndime, chirichonse cha zinthu zimenezo. Ubatizo, ife timaukhulupirira iwo. “Pali chiyembekezo chimodzi, Ambuyo mmodzi, Chikhulupiriro chimodzi, Ubatizo umodzi.” Ife timakhulupirira kuti pali ubatizo. Ife timakhulupirira mu chiukitsiro cha akufa. Mwamtheradi. Ife timakhulupirira kuti Yesu anafa ndipo anauka kachiwiri. Ife timakhulupirira zimenezo. “Kusanjika manja, pa odwala,” ndizo zomwe zinanenedwa. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Ife timakhulupirira zimenezo.

Koma izo ndi chiani? Paulo anati, “Zonsezo ndi ntchito zakufa.” Ndi chinachake chomwe inu mumachita.

107 “Tsopano tiyeni tipite mu ungwiro.” O, mai! Ife tikubwera mu Kachisi, osati maziko; Kachisi, Kachisi Iyeyemwe. Awo ndi maziko: lamulo, ndi chirungamo, n—n—n—ndi kujowina mpingo, ndi kubatizidwa, n—ndi kusanjika kwa manja. Zonsezo ndi madongosolo a mpingo.

“Koma tsopano tiyeni tipite mpaka mu ungwiro.” Ndipo pali Mmodzi yekha yemwe anapangitsidwa wangwiro, ameneyo ndi Yesu.

108 Kodi ife timalowa chotani mwa Iye? “Kupyolera mu Chimethodisti?” Ayi. “Chipentekoste?” Ayi. “Chibaptisti?” Ayi. “Kudzera mu mpingo uliwonse?” Ayi. “Roma Katolika?” Ayi.

109 Ife timalowa chotani mwa Iwo? Aroma 8:1.

Palibe chotero tsopano kutsutsidwa kwa iwo amene ali mwa Khristu. . . omwe samayenda motsatira zinthu za mdziko lino, thupi, koma motsatira zinthu za Mzimu, omwe samalabadira ku zomwe dziko liri nazo kuti linene.

110 Ngakhale iwe ukudwala, adokotala nkuti, “Iwe ufa,” iwe sumapereka tcheru kwa izo, sizimakusokoneza iwe pang’ono.

111 Ngati iwo akuuza iwe, “Iwe uyenera kukhala wa Chikatolika iwe usanapulumsidwe, kapena wa Chipresbateria, kapena uyenera kuti uchite *izi*,” iwe sumapereka tcheru kwa izo.

“Chotero palibe kutsutsidwa kwa iwo omwe ali mwa Khristu Yesu, omwe samayenda motsatira thupi, zinthu zomwe iwo amaziwona.” Chirichonse chomwe inu mumachiwona ndi maso anu ndi cha padziko lapansi.

112 Koma ndi zinthu zomwe inu mumaziwona mwa mzimu wanu, kudzera mu Mawu! Mawu ndiwo kalilole wodziyang’anirapo wa Mulungu yemwe amanyezimiritsa chomwe Iye ali ndi chimene inu muli. Aleluya! O, mai!

Iye amakuuzani inu. Ili ndi Bukhu lokha mu dziko lomwe limakuuzani inu komwe inu mukuchokera, yemwe inu muli, ndi kumene inu mukupita. Ndisonyezeni ine tsamba lililonse la zolemba, kulikonse, liri ndi sayansi yonse kapena china chirichonse, bukhu labwino lililonse lomwe linalembedwapo, palibe lililonse la iwo lingakuuzeni inu zimenezo. *Ili* ndi kalilole wodziyang'anirapo wa Mulungu, limene limakusonyezani chomwe Iye ali ndi chimene inu muli. Ndiye, pakati pakepo pali mzere wa Magazi, womwe umasonyeza chimene inu mungakhoze kukhala ngati inu mukufuna kuti musankhe. Ndi inu apo.

113 “Mwa Mzimu umodzi,” tsopano, Akorinto Woyamba 12. Kodi ife timalowa chotani mu Thupi limenelo?

“Pogwirana chanza?” Ayi, bwana. “Pa kujowina mpingo?” Ayi, bwana. “Pobatizidwa chammbuyo, cha mtsogolo? Mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera? Dzina la Yesu Khristu? Dzina la Rozi waku Sharoni, Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa? Chirichonse chomwe inu mukuchifuna?”

Izo ziribe chochita ndi ichi. “Yankho basi la chikumbumtima chabwino kwa Mulungu.” Ndipo komabe ife timakangana, ndi kukwiirana, ndi kutsutsana, ndi kugawikana, ndi kupanga zotisiyanitsa. Ndiko kulondola. “Koma izo zonse ndi ntchito zakufa.” Ife tikupita ku ungiro.

114 Izo ndi zinthu zomwe ine ndazichita. Mtumiki anakubatzani inu. Kaya iye anakubatzani inu cha nkhope mtsogolo, chammbuyo, kapena nthawi zitatu, nthawi zinai, kapena nthawi imodzi, kapena momwe iye anachitira izo, izo ziribe kanthu kochita ndi Icho. Inu mumangobatizidwira mu chiyanjano cha mpingo umenewo, mulimonse, kutsimikizira kwa mpingo uwo: inu mumakhulupirira imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Khristu. Kusanjika kwa manja, kuti muchize odwala, ndizo zodabwitsa, koma, izo zonse ndi zachibadwa, ndipo thupi limenelo lidzafanso motsimikiza basi monga momwe inu muliri a moyo. Ilo lidzafanso. “Tsopano tiyeni tiyike pambali zinthu zonse izo, ndipo tiyeni tipite mpaka ku ungiro.”

115 Kodi ife timafika bwanji ku ungiro? Ndi chimene ife tikufuna kuti tichidziwe.

. . . *Khristu watipanga angwiro* . . .

“Mulungu anaika pa Iye kusaweruzika kwa ife tonse. Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ndilo Thupi lomwe ife tikufuna kuti tifikoko. Ilo ndi Thupilo. Bwanji? Ngati inu muli mu Thupi limenelo, inu simudzawona konse chiweruzo, inu simudzalawa konse imfa. Ndinu mfulu kwa zonse za imfa, chiweruzo, tchimo, ndi china chirichonse, pamene inu muli mu Thupi limenelo.

116 “Kodi inu mumalowa chotani mu Ilo, mlaliki? Pojowina kachisi uyu?” Inu mwataika, apobe. Simungakhoze kujowina, mulimonse; ife tiribe bukhu lirilonse. “Ife timalowamo chotani mwa Ilo? Pojowina mpingo wina?” Ayi, bwana. “Ife timalowa chotani mu Ilo?” Inu mumabadwira mu Ilo.

117 Akorinto Woyamba 12.

Pakuti mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira mu thupi limodzi, . . .

118 Mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, ife timabatizidwa kulowa mu Thupi limenelo, ndipo ndife omasulidwa kwa tchimo. Mulungu samakuwonani inu aponso; Iye amangomuwona Khristu. Ndipo pamene inu muli mu Thupi limenelo, Mulungu sangakhoze kuliweruza Thupi limenelo. Iye analiweruza kale Ilo. Iye anatenga ziweruzo zathu ndipo anatiyitanira ife umo. Ndipo mwa chikhulupiriro, kupyolera mu chisomo, ife timalowamo, kumavomereza kukhululukidwa kwathu. Ndipo Mzimu Woyera umatibweretsa ife mu chiyanjano ichi limodzi ndi Iye. “Ndipo ife sitimayendanso motsatira zinthu za mdziko, koma ife timayenda mu Mzimu.”

Tinafulumizitsidwa, Mawu anadza kwa ife. Iye anafa mmalo mwanga. Ine ndapangidwa kukhala wamoyo. Ndi ine pano, yemwe nthawiyina ndinali wakufa mu tchimo ndi zolakwa, ndapangidwa wamoyo. Zokhumba zanga zonse ndi kuti ndizimutumikira Iye. Chikondi changa chonse chiri kwa Iye. Mayendedwe anga onse ndikufuna kuti akhale mu Dzina Lake. Kulikonse kumene ine ndipita, chirichonse chomwe ine ndichita, ine ndikumulemekezetsa Iye. Ngati ine ndikusaka, ngati ine ndikusodza, ngati ine ndikusewera mpira, ndi chirichonse chomwe ine ndikuchita, ine ndiyenera ndikhale, “Khristu ali mwa ine,” mu moyo woterowo, womwe ungawapangitse amuna kukhumba kuti akhale mwanjira imeneyo; osati kulongolola, kuchita miseche, ndi kukangana pa za mipingo yanu. Inu mukumvetsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

“Mwa Mzimu umodzi ife timabatizidwa kulowa mu Thupi limenelo.” “Ndipo pamene ine ndiwona Magazi, Ine ndizidutsa pa inu.”

119 Mvetserani. Tiyeni tiwerenge mopitiriza pang’ono apa, chonde.

. . .chomwe sichikanati chimupange wobwerakoyo kukhala wangwiro.

Pakuti ndime ya 2, mutu wa 10.

Pakuti ndiye izo sizikanati zisiyitsidwe kuperekedwa nsembe?

120 Ngati izo zikanakhoza kumupangitsa munthu kukhala wangwiro. . .Ndipo Mulungu akufuna ungwiro. Ngati kusunga malamulo, ngati kuchita malamulo onsewo, zingakupangeni

inu kukhala wangwiro, ndiye pali—palibe chifukwa chokhalira ndi china chirichonsenso; inu munapangidwa kale angwiro. Chifukwa, pamene inu muli wangwiro, ndinu Wamuyaya. Chifukwa, Mulungu ali mmodzi yekha yemwe ali Wamuyaya, ndipo ngati Mulungu ali mmodzi yekha wangwiro. Ndipo njira yokha yomwe inu mukanakhoza kukhalira Wamuyaya, ndi kukhala gawo la Mulungu. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

. . . *akatsukidwa kamodzi ayenera kukhala . . .
opandanso chikumbumtima cha tchimo.*

Chiani? “Wopembedza akatsukidwa kamodzi, samakhalanso ndi chikumbumtima . . .” Ngati inu mukulemba kumasulira kwa icho, ndi “chikhumbo.”

. . . *wopembedza akatsukidwa kamodzi . . .
samakhalanso ndi chikhumbo cha tchimo.*

. . . *ngati wopembedza anali atatsukidwa kamodzi . . .*

¹²¹ Inu mukamapita apo tsopano ndi kumati, “O, alaluya, ine ndinapulumsidwa usiku watha. Koma, chabwino, Mulungu adalitsike, *mkaziyu* wandipangitsa ine kubwerera mmbuyo. Alaluya, tsiku lina ine ndidzapulumutsidwa kachiwiri.” Iwe mbuli yosauka yosaphunzitsidwa. Umo si momwe izo ziliri.

¹²² “Wopembedza akatsukidwa kamodzi samakhalanso ndi chikumbumtima cha tchimo,” Baibulo linatero. Mvetserani, pamene ife tikuwerenga mopitirira, miniti yokha.

*Koma mu nsembe izo . . . munga anakumbukira
tchimo pachaka.*

¹²³ Tsopano ife tikuti titsikire mmusi, kuti tikakhudze cha pa ndime ya 8, kuti tisunge nthawi, ndi kumene ine ndikufuna kufikako.

*Pamwambapo ndiye pamene iye anati, Nsembe
ndi zopereka ndi zopereka zopyereza . . . za
tchimo inu simumazifuna, ngakhalenso kuti inu
mumakondweretsedwa nazo; zimene zinkaperekedwa
mwa lamulo;*

¹²⁴ Ndime ya 9.

*Ndiye iye anati, Taonani, ine ndikubwera kudzachita
chifuniro chanu, O Mulungu. Iye akuchotsapo . . .
kutenga . . . Iye akuchotsapo choyamba lamulo, kuti iye
akhoze kukhazikitsa chachiwiricho.*

¹²⁵ Ndikukhumba ife tikanakhala ndi nthawi kuti tikhale pa izo. Utali wonse womwe inu muli wa Chipresbateria, kapena wa Chipentekoste, kapena wa Chibaptisti, kapena wa Chimethodisti, Iye sangakhoze kuchita nanu kanthu. Iye ayenera kuti achotsemo zonsezo, poyamba, mukuona, chotero Iye akhoze kukhazikitsa chachiwiricho. Utali wonse inu mukuti,

“Chabwino, ine ndine wa Chimethodisti.” Aha, ndiribe kanthu kotsutsana ndi Achimethodisti, kapena Achibaptisti, kapena Achipentekoste. Koma, m’bale, izo si—sizinena za icho. Inu muyenera kuti mupitirire mpaka ku ungiro, umo ndi mwa Khristu.

¹²⁶ Penyani izi tsopano, miniti yokha.

Mwa womwe...ife timayeretsedwa kudzera mu kupereka nsembe kwa thupi la Yesu Khristu kamodzi kwa zonse.

¹²⁷ Aha? Tiyeni tingowerenga mopitirira pang’ono pokha, ndipo gwirani apo. Mulole izo zilowerere mkati pamene ife tikuwerenga, “Kamodzi kwa zonse.”

Ndipo wansembe aliyense pakuima tsiku ndi tsiku akutumikira kupereka nthawizonse nsembe yomweyo, imene siingakhoze konse kuchotsa tchimo:

Koma munthu uyu, . . .

Kodi inu mwakonzeka? Muli ndi chikhotho chanu mutachimasula tsopano, kotero kuti izo zisazembe, izo zipite mpaka mu mtima momwe? “Koma Munthu uyu.” Munthu wuti? Osati papa waku Roma, osati bishopu wa mpingo wa Chimethodisti, kapena mpingo wina uliwonse.

Koma munthu uyu, Khristu, atatha kupereka nsembe imodzi ya tchimo kwanthawizonse, anakhala pansu pa dzanja lamanja la Mulungu;

Kuchokera apa mpakana akuyembekezera kufikira adani ake apangidwe choponderapo phazi lake.

Penyani. Apa iye akubwera.

Pakuti mwa kupereka kumodzi iye watipanga a-n-g-w-i-r-o, iye watipanga angwiro . . .

“Mpaka chitsitsimutso chotsatira?” Kodi apo ati chiani?

. . . iye wawapanga angwiro kwanthawizonse iwo omwe ayeretsedwa.

Kodi inu mukumvetsa izo? “Tiyeni ife tipite mpaka ku ungiro.”

¹²⁸ Tsopano inu anthu achiyero mumati, “O, eya, ife timakhulupirira mu chiyero. Aleluya! Ife timakhulupirira mu kuyeretsedwa.” Koma inu mukutenga zanu zanu. Inu mumangosiya izi ndi kusiya izo. Inu mukudziwa kuti inu simukuyenera kuti muzichita izo.

Kupatula ngati Khristu watsegula chitseko ndi kufulumizitsira izo kwa mtima wanu, ndipo inu mwakhala malo omwe tchimo liri lakufa, ndi chikhumbo, zonsezo zitapita. Ndiye, Iye amachotsapo chirungamo chanu chanucho, kuti Iye akhoze kudzikhazikitsa Yekha mwa inu. “Ndipo uyo ndi

Khristu, Mwana wa Mulungu, mwa inu, chiyembekezo cha Ulemerero.”

... *tiyeni ife tipite mpaka ku ungwiro;*

129 Kodi ife tingakhale bwanji angwiro? Kupyolera mu imfa ya Khristu. Osati kupyolera mu kujowina mpingo. Osati kupyolera mu ntchito zathu zabwino, zomwe ife timachita. Izo zonse ndi zabwino. Osati chifukwa ife tinabatizidwa mwanjira *iyi* kapena mwanjira *iyu*. Osati chifukwa ife tinachiritsidwa, posanjikidwa manja. Osati chifukwa cha zinthu zina izi, “Ife timakhulupirira mu imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro.”

130 Paulo anati, “Ine ndikhoza kuyankhula ndi lirime longa la anthu ndi Angelo,” ndiwo onse malirime omwe amamvetsedwa ndi malirime omwe sangakhoze kumvetsedwa, ayenera kuti atanthauziridwe, “Ine sindiri kanthu. Ngakhale ine ndikhale nayo mphatso ya chidziwitso ndi kumamvetsa nzeru yonse ya Mulungu,” kukhoza kumalifotokoza Baibulo, kuchokera... kulimangiriza ilo palimodzi, “Ine sindiri kanthu.” Sizimachita ubwino wochuluka kupita ku sukulu ndiye, sichoncho, kuliphunzira Baibulo? “Ngakhale ine ndikhale ndi chikhulupiriro kuti ine ndizikhoza kumasuntha mapiri...” Misonkhano ya machiritso siitanthauza mochuluka kwambiri ndiye, sichoncho iyo? “Ine sindiri kanthu, ngakhale ine ndipereke thupi langa kuti aliwotche ngati nsembe.”

131 “O,” iwo angati, “munthu ameneyo ndi wachipembedzo.”

132 “Koma iye si kanthu,” Paulo anatero, “simunakhale kanthu konse.”

133 “Pakuti pamene pali malirime, iwo adzaleka; pamene pali mauneneri, iwo adzalephera; pamene pali zinthu zina zonse izi, izo zidzalephera. Koma pamene icho chomwe chiri changwiro chidzabwera, chomwe chiri chamderamdera chidzathetsedwa.” Mukuona, “changwiro” icho. Kodi changwiro ndi chiani? Chikondi. Chikondi ndi chiani? Mulungu. “Tiyeni ife tiyike pambali ntchito zonse zazing’ono zakufa izi ndi malangizo, ndipo tipite mpaka ku ungwiro.” Inu mukuziona izo? Ife timakhala angwiro kupyolera mwa Khristu. Kodi ife timalowa bwanji mwa Iwo? Mwa ubatizo wa Mzimu Woyera.

134 “Chabwino, chimachitika ndi chiani?” Inu mumadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.

135 “Chabwino, kodi ine ndizigwedeze, ndilumphe, pochita izo?” Inu, inu simukusowa kuti muchite chirichonse. Inu mwachita kale izo, Mulungu wakubweretsani inu kuchokera ku imfa kudzafika ku Moyo, ndipo ndinu wamoyo. Ndiye zipatso zanu za moyo wanu zikusonyeza izo.

136 Ambiri a inu Achimethodisti ndi Anazerene munafuula molimba basi momwe inu mukanathera kufuula, nkumaba

chimanga mmunda wa munthu, ndiko kulondola, kuchita chirichonse chomwe inu mukanakhoza.

¹³⁷ Ochuluka a inu Achipentekoste munayankhula mu malirime, ngati kutsanulira nandolo pa chikopa cha ng'ombe, zedi, munatuluka kunja komwe ndipo munathawira kwina ndi mkazi wa mwamuna wina, munakachita mitundu yonse ya zinthu. Izo sindizo ayi, m'bale.

¹³⁸ Musati muyesere kuti mukhale ndi kumverera kulikonse kapena chirichonse choti chitenge malo a Mzimu Woyera. Pamene Kubadwa kwatsopano kubwera, inu mumasinthidwa. Inu simumasowa kuti muchite chinachake kuti mutsimikizire izo. Moyo wanu umatsimikizira izo, pamene inu mukuyenda. Chikondi chanu, mtendere, kupirira, kuleza, kufatsa, chipiriro. Ndizo zomwe inu muli, ndipo dziko lonse limawona chinyezimiritsa cha Yesu Khristu mwa inu.

¹³⁹ Tsopano, kuyankhula mu malirime, kufuula mmenemo, izo ndi zotsatira chabe zomwe zimatsatira Moyo wa mtundu uwu.

Ndipo inu mukhoza kutenga, kusanzira zotsatira izo, ndi kusakhala nawo konse Moyo umenewo. Ife timaziwona izo. Ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndithu, inu mukudziwa. Ndithudi, moonadi inu mukudziwa. Mai! Inu mumaziwona izo konse mozungulira inu.

¹⁴⁰ Chotero, palibe kanthu komwe inu mungathe kunena kuti ndi umboni wa Mzimu Woyera, kupatula utakhala moyo umene inu mukuukhala. Tsopano, ngati inu mukufuna kuti muyankhule ndi malirime, izo ndi zabwino mwangwiro ngati inu mukukhala moyo woyikira izo kumbuyo. Ndiko kulondola. Ndipo ngati inu mukufuna kuti mufuule, zabwino, izo ndi zabwino. Ine ndimafuula, nanenso, ndimafika posangalala kwambiri nthawizina ine ndimalephera kuvala nsapato; ine ndimakhala ngati ndilumphepo. Ndipo izo ndi zodabwitsa. Ine ndimakhulupirira izo.

¹⁴¹ Ine ndawonapo masomphenya, ndi odwala kuchizidwa, akufa nkuuka. Pamene iwo amagona kunja uko ndipo madotolo nkuchokapo ndi kuti, "Iwo atha ndipo apita," atagona pamenepo maora angapo; ndipo Mzimu Woyera nkubwera apo pomwe ndi kusonyeza masomphenya, kupita uko ndi kukamuutsapo munthu ameneyo. Ine ndawawonapo iwo omwe ali ogontha, osayankhula, ndi akhungu, ndi olumala, akuyenda. Izo sindizo . . . Izo ndi zotsatira chabe.

¹⁴² M'bale, nthawi ina kale, dziko lisanakhale konse ndi maziko kwa ilo; Mulungu kupyolera mu chisomo Chake Chamuyaya, Iye anayang'ana pansu, ndipo mwakudziwiratu Iye anakuwonani inu ndi ine. Iye anadziwa m'badwo umene ife tikanadzakhalamo. Iye ankadziwa chomwe ife tikanadzakhala tiri. Chotero, mwa

kusankha, Iye anatisankha ife asanaikidwe maziko a dziko, kuti tidzakhale ndi Iye opanda banga.

¹⁴³ Tsopano, ngati Iye anatisankha ife asanaikidwe maziko a dziko kuti tidzakhale mwa Iye opanda banga, ndipo ife tinabadwa yense wa mabanga, ndipo palibe kalikonse kangathe. . . palibe komwe kangatiyeretse ife, ife tidzakhala bwanji wopanda. . . ife tikhala bwanji opanda banga? “Iye anamutumiza Mwana wake yekha wobalidwa, kuti aliyense yemwe angakhulupirire mwa Iye asadzakhale ndi mapeto a moyo, koma adzakhale nawo Moyo Wamuyaya; asadzawonongeke konse, koma adzakhale nawo Moyo Wamuyaya.” Ndiye pamene ife tibwera kwa Iye, mwa chikhulupiriro, kupyolera mu chisomo ife timapulumsidwa, mwa Mzimu Woyera ukuitana kwa ife.

¹⁴⁴ Pasanakhale konse thupi pa dziko lino, matupi anu anali ali kuno. Iwo anapangidwa ndi kashiamu, potashi, chinyezi, kuwala—kuwala kwa dziko, mafuta, ndi zina zotero, zipangizo zikisitini. Ndipo Mzimu Woyera unayamba kufungatira pa dziko lapansi, “kukopa.” Ndipo pamene Iwo unatero, chinthu choyamba inu mukudziwa, panatulukira duwa laling’ono la Isitara. Ndiye Iye anafungatirapo udzu wina, ndi mbalame zina, ndipo patapita kanthawi, munthu anatulukirapo.

¹⁴⁵ Tsopano, Iye sanamupange konse mkazi kuchokera mu fumbi la dziko lapansi. Iye anali kale mwamuna, pakuyamba pomwe; mwamuna ndi mkazi ali mmodzi. Chotero Iye anatenga kuchokera ku mbali ya Adamu, nthiti, ndipo anapanga mkazi, wothandizira kwa iye. Ndiyeno tchimo linabwera umo. Ndiye tchimo litabwera umo. . .

¹⁴⁶ Ndipo Mulungu sadzagonjetsedwa, ziribe kanthu zomwe zingachitike. Iye sadzagonjetsedwa konse. Kenako, akazi anayamba kubala anthu padziko lapansi. Ndipo Mulungu, kudzera mu chisomo Chamuyaya, anawona yemwe akanati adzapulumutsidwe, ndipo Iye anakuitanani inu. “Palibe munthu angadze kwa Ine, kupatula Atate Anga atamuitana iye, poyamba.” “Osati iye amene afuna, kapena iye amene athamanga, koma Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.”

¹⁴⁷ Inu mukuti, “Chabwino, ine ndinamufunafuna Mulungu. Ine ndinamufunafuna Mulungu.” Ayi, inu simunatero. Mulungu anakufunanifunani inu. Ndi momwe izo zinaliri pachiyambi.

¹⁴⁸ Sanali Adamu akuti, “O Atate, Atate, ine ndachimwa. Kodi Inu muli kuti?”

¹⁴⁹ Izo anali Atate akuti, “O Adamu, Adamu, iwe uli kuti?” Icho ndi chikhalidwe cha munthu. Uwo ndi mtundu wa munthu. Ndi momwe iye anapangidwira.

¹⁵⁰ “Ndipo palibe munthu angadze kwa Ine kupatula Atate atamukoka iye. Ndipo onse omwe Atate anandipatsa Ine. . .” Aleluya! “Onse omwe abwera, ine ndidzawapatsa iwo Moyo

Wamuyaya, ndipo ndidzamuutsa iye pa tsiku lotsiriza.” Lodala lakelo, lonjezo lodala lakelo, la Mulungu wa Kumwamba! Pomwe ife titi tifikepo usikuuno, kuti, “Iye analumbira pa Iyeyekha.” Palibe wina wamkulupo. Iwe umalumbira pa wina wamkulu kuposa iwe. Palibe wina wamkulu, chotero Mulungu anatenga lumbiriro kwa Iyemwini. Ife tikufika mu izo, momwe Iye anachitira izo ndi pamene Iye anachitira izo; ndipo anatenga lumbiriro kwa Iyemwini, kuti Iye akanadzatzidzutsa ife apo ndi kutipanga ife chuma Chake chomwe.

¹⁵¹ O, ungwiro wake ndi kulimba komwe ife tingaimepo, mmawa uno! Momwe inu mungayang’anire, ngati imfa ikuyang’ana pa inu mu nkhope momwe, inu mukhoza kunena monga Paulo, “Imfa, ilikuti mbola yako? Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Koma mathokozo akhale kwa Mulungu, Yemwe akutipatsa ife chigonjetso kupyolera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Ndi inu apo. Bwanji?

¹⁵² “O, inu munachita *zakuti-n-zakuti*.”

¹⁵³ “Ine ndikudziwa izo, koma ine ndaphimbidwa ndi Magazi Ake.” Aleluya!

¹⁵⁴ “Mwa Mzimu umodzi, ife tonse tinabatizidwira mu Thupi limodzi.” Inu Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, chirichonse chomwe inu muli, ife tinabatizidwira mu Thupi limodzi. Ife tiri nacho chiyanjano, ndipo ndife mbadwa za Ufumu wa Mulungu, tikudzinenera, kuti, “Ife sitiri a mdziko lino.”

¹⁵⁵ Msungwana wanga wamng’ono anabwera, tsiku lina, anati, “Adadi, msungwana wamng’ono uyu wachita *zakuti-n-zakuti*. Ndipo iwo anachita *zakuti-n-zakuti*. Ife tinapita kunyumbako. Iwo anachita *zakuti-n-zakuti*.” Ine ndinati. . . anati, “Chifukwa chiani ife sitimachita zimenezo?”

¹⁵⁶ Ine ndinati, “Wokonedwa, ife sitiri a mdziko limenelo. Iwo amakhala mu dziko kwa iwoeni.”

¹⁵⁷ Anati, “Kodi ife sitimayenda pa nthaka yomweyi.”

¹⁵⁸ Ine ndinati, “A mdziko, wokonedwa. Ife sitiri a anthu amenewo.”

¹⁵⁹ Baibulo linati, “Tulukani kwa iwo, khalani inu olekanitsidwa,” atero Mulungu. Mukuona, inu simuli a limenelo. Ndiyeno pamene Chikhalidwe chatsopano icho chibwera mwa inu, inu simumasowa kuti muzikokedwa. Inu simumafuna kuti mubwerere mmbuyo, monga mkazi wa Loti. Inu mwangobadwa, kuchokera mwa ilo. Ndipo inu muli mu dera lina. Ndipo izo zikuwoneka za nyansi kwa inu.

Ndipo uyu, Amereka wamkulu, wopambana uyu yemwe ife tiri kukhalamo, wasanduka chisokonezo chimodzi chachikulu cha izo. Chirichonse chiri kukhumbira ndi akazi. Ndipo akazi momwe iwo akuvalira, amuna momwe iwo akuchitira, n—

ndi zinthu zomwe iwo akuchita, ndiyeno nkumadzitcha okha, “Akhristu.”

¹⁶⁰ Mwa chitsanzo, Elvis Presley uyu, wapita ndi kukajowina mpingo wa Chipentekoste tsopano. Zoono, ndi komwe Yudasi analandira zidutswa makumi atatu za siliva. Elvis ali ndi mndandanda wa Makadilaki, n—ndi madola mamilioni angapo, pa kugulitsa ufuluwakubadwa nawo wake. Arthur Godfrey. Tayang’anani pa izo.

¹⁶¹ Tayang’anani kuno pa Jimmy Osborne mu Louisville, kunja uko ndi bugii-wugii wakale, roke-n-rolo, zammimba zovunda zakale ndi nyansi. Ndipo Lamlungu mmawa, nkutenga Baibulo ndi kuima pansanja ndi kumalalikirira. Chamanyazi chakecho!

Palibe zodabwitsa Baibulo linati, “Gome lirilonse ladzaza ndi masanzi.” Pakuti, ife tikukhala mu tsiku lowopsya!

¹⁶² Ndipo anthu amati, “O, iwo ndi achipembedzo kwambiri.” O! Kodi inu simukudziwa kuti Mdierokezi ndi wachipembedzo? Kodi inu simukudziwa kuti Kaini anali wachipembedzo basi monga Abele analiri? Koma, iye analibe Vumbulutso. Ndi zimenezo. Iye analibe Vumbulutso.

Eya, ife tonse timapita ku mpingo, koma alipo ena omwe ali nawo Moyo, ndi omwe ali nalo Vumbulutso la Yesu Khristu mu mtima mwawo. Osati pakugwirana chanza, pakulumpha, osati pojowina mpingo. Koma, Vumbulutso, Mulungu wamuulula Iye.

¹⁶³ Tayang’anani zomwe ananena, “Kodi anthu amati ine, Mwana wa munthu, ndi ndani?”

¹⁶⁴ “Ena amati Ndinu ‘mneneri.’ Ndipo ena amati Ndinu ‘Eliya.’ Ndipo ena . . .”

Anati, “Koma inu mukuti ndi ndani?”

¹⁶⁵ Petro anati, “Ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.” Izo sizinali zochokera pa milomo yake.

¹⁶⁶ Iye anati, “Wodala ndiwe, Simoni, mwana wa Yonasi, pakuti thupi ndi magari sizinakuululire iwe izi. Iwe sunaziphunzire izi kwina—zongoganizira zina za Baibulo, kapena fioloje ina yaku seminare. Wodala uli iwe, pakuti thupi ndi magari sizinakuululire iwe izi. Koma Atate Anga omwe ali Kumwamba awulula izo. Ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka potsutsana ndi Iwo.”

¹⁶⁷ Ngati muli Mkhristu, mmawa uno, chifukwa ndinu a mu mpingo, inu mwataika. Ngati muli Mkhristu chifukwa inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo, ndinu mfulu kwa chiweruzo; mwalowa mwa Khristu, inu mukubwera mu ungwiro nthawi zonse. Mulungu sangakhoze kuwona chinthu chimodzi. Inu mukuti, “Chabwino, kodi ine ndizilakwitsa konse?” Zedi, koma inu simumachita izo mwadala.

168 Tsopano ife tifika mu zimenezo, mu maminiti pang'ono okha, “Pakuti iye amene amachimwa mwadala atalandira kale chidziwitso cha Choonadi, sipamakhalanso nsembe ya kwa tchimolo.” Ife tifika mu zimenezo usikuuno, chifukwa tachedwa pang'ono tsopano.

169 Tiyeni tiwerenge ndime zingapo zokha za izi, kuti ife tikhoze kumverera bwinoko pofika pansi mochulukira pang'ono. Chabwino. Chabwino, ife tiyambira kumene pa zimenezo usikuuno, ndime ya 4. Mvetserani kwa izi.

Pakuti ndi kosatheka kwa iwo omwe anaunikiridwapo kamodzi, ndipo anapangidwa... ndipo akhala... ndipo analawapo za mphamvu, mphatso zakumwamba, ndipo anapangidwa kukhala otenga nawo mbali ndi Mzimu Woyera,

Ndipo... analawa mawu abwino a Mulungu, ndi mphamvu ya dziko likudza,

Ngati iwo angati agwere kwina, kuti adzikonzere iwoeni... ku kulapa;...

Mukuona? Ndipo tizitengera izo ku Ahebri 10, ndipo mmbuyo ndi mtsogolo, kuti tisonyeze chomwe izi ziri.

170 Amzanga, “Tiyeni ife tipite mpaka ku ungwiro.” Ife tiri... ife sitiri... Ife tiribe chowiringula lero. Ife tiribe chowilingula, konse. Mulungu wa Kumwamba wawonekera mu tsiku lotsiriza lino ndipo akuchita zinthu zomwezo zimene Iye ankazichita apo, pamene Iye anali kuno kalelo, pamene Iye anali padziko lapansi. Iye watsimikizira, pamene ife tikubwera kudutsa mu Baibulo ili. Ndipo i—inu, kalasi, mukudziwa izi, kuti ife tatenga chozizwitsa mwa chozizwitsa, ndi chizindikiro mwa chizindikiro, mwa chodabwitsa ndi chodabwitsa, zomwe Iye ankachita ndi ana mu chipululu, zinthu ndi zizindikiro zomwe Iye ankachita; zinthu zomwe Iye ankachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, akuwonetseredwa mu thupi; ndipo zinthu izo zomwe zikuchitika lero, pomwe pano pakati pathu. Mawu ali pano kuti atsimikizire izo. Pano pali chinthu choti chinene kuti ndi zolondola, kuti achipange icho kukhala cholondola. Pano pali Mzimu wa Mulungu woti uzichita chinthu chomwecho, chotero ife tiri opanda chowiringula.

Tiyeni ife tipemphere.

171 Atate Akumwamba! Powona kuti ife tazunguliridwa mmbalimu ndi unyinjira wawukulu chotero wa mboni, tiloleni ife tiike kumbali mawu aliwonse, chirichonse,” cholakwika chirichonse, mawu oyipa aliwonse, mawu olankhulidwa-moipa aliwonse, lingaliro lirilonse, “ndipo tiloleni ife tithamange ndi chipiriro liwiro lomwe laikidwa patsogolo pathu, kuyang'ana kwa woyambitsa ndi wotsirizitsa wa chikhulupiriro chathu, Ambuye Yesu Khristu.” O lidalitsike Dzina Lake loyera losafanizitsidwalo! Momwe Iye anadzera ku dziko lapansi kuti

adzawaombole anthu okugwa, ndi kuwabweretsanso iwo ku chiyanjano cha Ambuye Mulungu. Ndipo ife tikukuthokozani Inu pa izi. Ndipo tsopano mwa chisomo Chake...Ife sitinamusankhe konse Iye, koma Iye anatisankha ife. Iye anati, “Inu simunandisankhe Ine, koma Ine ndinakusankhani inu.” Liti? “Asanaikidwe maziko a dziko.”

¹⁷² Ndipo, wokonedwa Mulungu, ngati alipo ena omwe akhala pano mmawa uno, mwinamwake omwe amaziika kumbali izi kwa zaka ndi zaka, koma mowirikiza pali kugogoda kwakung’ono pa mtima wawo. Mwinamwake iwo anajowina mpingo, kuganiza, “Chabwino, izo zikhala bwino.” Atate, zedi, Malemba afotozoza izo mmawa uno: kuti iwe sungakhoze kubisala kuseri kwa mpingo, ndi kukhala wolungama; ngakhalenso iwe sungakhale wabwino, wosanama ndi wosaba ndi kumachita chirichonse moipa, ndipo nkukhalabe wolungama.

¹⁷³ Alipo wolungama mmodzi yekha yemwe ife tiri naye, osati cha ifeeni, koma chirungamo Chake. Iye anachipangitsa chipulumutso chathu kukhala changwiwo. Chotero, pokhala mwa Iye, Mulungu samawona zolakwitsa zathu. Pamene ife tichita chirichonse cholakwika, pali mzimu mwa ife umene umafuulira uko, “O Atate, ndikhululukireni ine!” Ndiye Mulungu samaziwona izo. Ndizo...Ife timabweretsedwa mu chiyanjano ndi chisomo ndi Iye. Perekani izi, Ambuye, pamene ife tikutseka msonkhano uwo, mu Dzina la Khristu. Ameni.

¹⁷⁴ Kwa mphindi yokha, ine ndikufuna ndikufunseni inu. Ziribe kanthu zomwe inu mungachite, inu ndinu otayika. Mvetserani kwa izi. Nthawi yina kalepo...Ine mwina ndinazinenapo izo kale. Ichi ndi chondichitikira chaching’ono chomwe chinachitika kwa ine.

¹⁷⁵ Ine ndinali uko k—ku Toledo, Ohio. Ine ndinali mu chitsitsimutso n—ndipo ndinali ndi msonkhano kumusi uko ndi anthu ochulukwa kwambiri. Iwo ankadziwa mahotelo komwe ine ndinali; chotero iwo ananditengera ine ku midzi. Ine ndinkakhala kunjira uko, motelo yaing’ono.

¹⁷⁶ Ife tinali tikudya ku malo odyera aang’ono achi Dunkard. Iwo anali malo odabwitsa, madona aang’ono mmenemo owoneka Achikhristu ndi oyera monga iwo akanakhalira, ankhondo ndipo abwino kwenikweni. Litafika Lamlungu, ine ndinamva njala. Ine ndinali ndikusala pang’ono. Ndipo ine ndinafunika kuti ndiwoloke msewu kupita kwa ina, kukaitanitsa pang’ono. Msewu waung’ono apo pafupi ndi pangodya, ndipo apo panali malo achizolowezi, awamba, Achimereka pamenepo, oti nkukadyamo. Aang’ono, anali ndi malo aang’ono, malo a cafe, otsegulidwa usiku wonse. Pamene ine ndinalowa mmenemo Lamlungu ilo, pafupi thuu koloko madzulo, ndisanapite uko kuti ndikalalikire madzulo amenewo.

¹⁷⁷ Ine ndinali nditapezeka kwambiri, ine sindinadziwe choti ndichite. Ine ndinalowa umo, ndipo chinthu choyamba chomwe ine ndinazindikira chinali dona wamng'ono wa pafupi usinkhu wa zaka sikisitini, eitini, wokondedwa wina wa adadi, wokondedwa wina wa amayi, ataima kumbuyo uko ali ndi mnyamata, ali ndi manja ake cha mu chiuno mwake. Gulu la a mmatini ali pa—pa kauntala.

¹⁷⁸ Ine ndinamva makina olowetsa zinthu. Ndinayang'ana cha *apa*, ndipo apo panali wa polisi ataima pamenepo ali ndi manja ake atamugwira mkazi, mmwamba kuzungulira apa, mchiuno mwake, ndipo akusewera makina olowetsa zinthu. Tsopano, inu mukudziwa kuti njuga ndi makina olowetsa zinthu ndi zoletsedwa mu Ohio, inu anthu achi Buckeye kuno. Ndipo inu mukudziwa kuti izo ndi zoletsedwa. Ndipo apa panali lamulo, likusewera makina olowetsa zinthu; ndipo bambo wa usinkhu wanga, mwinamwake wokwatira, gulu la ana, mwinamwake gogo wamwamuna. Wa polisi, wokwera nakalondera, akusewera makina olowetsa zinthu. Apo panali wamng'ono uyo...Kodi wausinkhu wa mmatini ankachita chiani? Nchiani ichi chimachitidwachi?

¹⁷⁹ Ine ndinaima pamenepo. Palibe aliyense anandizindikira ine ndikulowa umo, iwo anali otanganidwa kwambiri, theka la iwo ataledzera. Kotero, ine ndinapenya. Ine ndinamumva wina akuti, “Chabwino, kodi inu mukuganiza kuti mvula iwononga mbewu yamasamba?” Ndipo ndinayang'ana pozungulira cha apa, ndipo apa panakhala dona atakhala pamenepo, dona wokalamba, kwenikweni...Iye anali sikisite faifi, sevente, pafupi nazo. Ndipo dona wosaukayo...Ine sindimamutsutsa aliyense pakuwoneka mwakupambana kwao. Koma pamene iye...Iye anali atadzikonza yekha, anali atapanga tsitsi lake mwa buluu, likuwoneka mwabululu weniweni. Ndipo lonse litayepulidwa, pamwamba, ndipo analipanga ilo mwabululu weniweni. Ndipo iye anali ndi zodzilocha zokhuthara kwenikweni, kapena chomwe inu mumazitcha zinthu zomwe anazipaka pa nkhope yake, ndi madontho aakulu. Ndipo iye anali atavala zazifupi zazing'ono kwambiri, ndipo chinthu chosauka chokalambacho chinali chamakwinya kwambiri mpaka nyama, yokwinyika, nyamayo inali ikulendewera pansu munga *chomwecho* pa miyendo yake. Ndipo iye anali ataledzera. Iye anali atakhala pamenepo ndi bambo wachikulire, mu nthawi ya chirimwe, atavala chimodzi cha zikhoto, zakale zaku nkondo zotuwa izi, kapena chikhotho cha olive. Icho chikulendewera munga *chomwecho*, ndi mpango wawukulu atawukolekera kuzungulira khosi lake. Ataledzera, awiri a iwo, ndipo iwo anali ndi mkazi wachikulire wosauka uyu.

¹⁸⁰ Ine ndinaima pamenepo ndipo ndinayang'ana pozungulira. Ine ndinati, “Mulungu, inu mukukhoza bwanji kupirira nazo izo? Ch—chotani...Inu mukuyang'ana chotani pa zonga

chonchozo? Pamene, izo zikundipangitsa ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo, kuganiza izo, mmotani—mungati Inu mukhoze kuyang’ana pa izo? Mwakuti, izo zikuwoneka ngati Inu mukanakhoza kuchiphulitsa chinthucho chitseguke. Kodi Rebekah wanga wamng’ono ndi Sarah adzayenera kudzabwera pansu pa mtundu uwo wa kukopa? Kodi asungwana anga aang’ono awiri adzati adzakomane ndi—kutchuka, kudziwika kotero, mdziko monga izo ziri lero, komwe anthu akuchitako monga choncho? Mulungu, ine ndingakhoze bwanji nkomwe. . . kodi ine ndingachite chiani?”

Ndithudi, ndi chisomo Chake. Ngati iwo anadzozedweratu ku Moyo Wamuyaya, iwo adzabwera kwa iwo. Ngati iwo sanali, iwo sadzatero. Ine sindikudziwa. Izo ziri kwa Mulungu. Ine ndichita gawo langa.

¹⁸¹ Ine ndinaganiza, “Inu mungakhoze bwanji kupirira nazo, Mulungu? Zikuwoneka ngati Ndinu woyera kwambiri mwakuti Inu mukanangochisesapo chinthu chimenecho pa dziko lapansi.” Ine ndinati, “Tayang’ana pa gogo wamkazi wosauka wakhala apoyo. Tayang’anani pa msungwana wamng’ono uyo kumbuyo uko. Ndipo apa pali mkazi wayima apo, mwinamwake usinkhu wa zaka twente faifi. Ndipo wa polisi uyo ali ndi mikono yake atamugwira mchiuno mwake, akusewera makina olowetsa zinthu. Ndipo apo pali lamulo; fukoli lapita. Apo pali umayi utapita. Apa pali wachikulire wapita. Ndipo apo pali msungwana wamng’ono wakhala kumbuyo uko, ndipo iye wapita. Tayang’anani pa anyamata, pamene iwo akuyenera kukhala ali mu mpingo kapena kwina kwake.”

¹⁸² Ine ndinati, “O Mulungu, kodi ine ndingachite chiani? Ndipo pano ine ndiri mu mzinda uno, ndikufuula ndi mtima wanga wonse, ndipo iwo akunyalanyaza izo ndi kumayenda ngati kuti iwo anali. . .” Ine ndinaganiza, “Chabwino, Mulungu?”

¹⁸³ Chabwino, ndiye lingaliro linadza, “Ngati Ine sindinawaitane iwo, iwo angabwere motani? Onse omwe Atate anandipatsa Ine adzabwera. ‘Inu muli nawo maso koma inu simukukhoza kupenya, makutu ndipo inu simukukhoza kumva.’”

¹⁸⁴ Ine ndinaganiza, “Chabwino, ngati Purezidenti akanabwera ku mzindawu mmalo mwa chitsitsimutso, aliyense akanabwera uko. O, zedi, izo ndi za chidziko.”

¹⁸⁵ Ndiye ine ndinayamba kuganiza, “Chabwino, Mulungu, bwanji Inu simukungo, chabwino, kubwera, kumutuma Yesu ndi kungoti tithane nazo izo? Simungangoti m—mungopita ndi kukathana nazo, ndi kuzilola izo zipite?”

¹⁸⁶ Ndiye ine ndinayamba kuwona chinachake chikusuntha kutsogolo kwa ine. Icho chinkawoneka ngati kamvuluvulu wamng’ono akuzungulira monga *chonchi*. Ine ndinapitirira kumuyang’ana iye. Ine ndinaliwona dziko likuzungulira

zungulira. Ine ndinaliyang'ana ilo, ndipo pamene ilo linali kupemerera chinachake uko. Ine ndinayang'ana, ndipo uko kunali kupemereredwa zofiira, Magazi ofiira, ponse, kuzungulira dziko; monga ngati kamvuluvulu akupita mozungulira, ngati nyenyezi, ndipo inali ndi chomazungulira monga *chonchi*. Ndipo ine ndinayang'ana pa kuzungulira uku. Ndipo basi pamwamba pa izo, ine ndinamuwona Yesu mu masomphenya. Iye anali akuyang'ana pansi. Ndipo ine ndinadziwona ndekha nditaima pansi apa pa dziko lapansi, ndikuchita zinthu zomwe ine sindimayenera kuti ndizichita. Ndipo nthawi iliyonse yomwe ine ndimachimwa, Mulungu akanati andiphe ine, “Chifukwa, tsiku lomwe iwe udzadya za iwo, tsikulo iwe udzafa.” Ndipo chiyero cha Mulungu ndi chilungamo chimafuna, ndipo iwe unkayenera kuti ufe. Ndiyeno ine ndinayang'ana kumeneko. Ine ndinkapitiriza kuisita maso anga. Ine ndinati, “Ine sindiri. . . Ine sindinapite kokagona. Ndine. . . Awa ndi masomphenya. Ine ndikutsimikiza awa ndi masomphenya.”

¹⁸⁷ Ine ndinapitiriza kuyang'ana, pamene ine ndinaima kuseri kwa chitseko. Ndipo ine ndinawaona machimo anga omwe akubwerapo. Ndipo nthawi iliyonse yomwe iwo ankayamba kuti agunde Mpando wachifumu, Magazi Ake ankachita ngati bampara pa galimoto. Iyo inkawagwira iwo, ndipo ine ndinkawawona Iwo akukutumulidwa, ndipo Magazi ankakhoza kuyenderera mmusi pa nkhope Yake. Ndipo ine ndinamuwona Iye akukweza manja Ake, ndi kuti, “Atate, mukhululukireni iye, iye sakudziwa zomwe iye akuchita.”

¹⁸⁸ Ine ndinadziwona ine ndekha ndikuchita chinachakenso, icho chinamugwedezanso Iye, bampu. Izo zikanati, Mulungu akadati andiphe ine apo pomwe, koma Magazi Ake anali kundigwira ine. Iwo anali kugwira machimo anga. Ine ndinaganiza, “O Mulungu, kodi ine ndinachita zimenezo? Zedi izo sindinali ine.” Koma izo zinali.

¹⁸⁹ Ndiye ine ndinapita ndikuyenda monga *chonchi*, ngati kuti ine ndinali kupita mu chipinda chimenecho, ndipo ine ndinayenda mpaka pafupi ndi Iye. Ine ndinawona bukhu liri pamene, ilo linali ndi dzina langa pa ilo, ndi mitundu yonse ya zilembo zakuda zitalembedwa pamenepo. Ine ndinati, “Ambuye, ine ndikupepesa kuti ndinachita izi. Kodi ndi machimo anga anakupangitsani Inu kuti muchite zimenezo? Kodi ine ndinamwaza Magazi Anu mdziko? Kodi i—kodi ine ndinachita izi kwa Inu, Ambuye? Ine ndikupepesa kwambiri kuti ine ndinachita izo.” Ndipo Iye anandifikira. Ine ndinati, “Kodi Inu mungandikhulukire ine? Ine sindinali kutanthauza kutero. Ine ndi. . . Inu, mwa chisomo Chanu, ine ndiyesera kuti ndikakhale ndiyamata wabwino ngati Inu mutangondithandiza ine.”

¹⁹⁰ Iye anatenga dzanja Lake ndipo anakhudza mmbali Yake, anatenga chala Chake ndipo analemba “wakhulukidwa” pa

bukhu langa; analiponyera ilo kumbuyo kwa Iye, Nyanja ya Kuiwalira. Ine ndinaziyang'ana izo pang'ono pokha. Ndipo Iye anati, "Tsopano, Ine ndakukhulukira iwe, koma iwe ukufuna kuti umuweruze mkaziyo." Mukuona? Anati, "Iwe wakhulukidwa, koma nanga bwanji iye? Iwe ukufuna kuti umuphulitsepo iye. Iwe sumafuna kuti iye akhale moyo."

¹⁹¹ Ine ndinaganiza, "O Mulungu, ndikhulukireni ine. Ine sindimatanthauza kuti ndiganize zimenezo. Ine sindimafuna kuti ndichite izo. I—i—ine sindimafuna kuti ndichite izo."

¹⁹² "Iwe wakhulukidwa. Iwe ukumverera bwino yense. Koma nanga bwanji iye? Iye akusowa chimenecho, nayenso. Iye akuchisowa icho."

¹⁹³ "Chabwino," ine ndinaganiza, "Mulungu, ine ndingadziwe bwanji yemwe Inu mwamuitana, ndi yemwe Inu simunamuitane?" Iyo ndi ntchito yanga kuti ndiziyankhula kwa aliyense.

¹⁹⁴ Kotero, pamene masomphenya anandichokera ine, ine ndinayenda kupita kwa iye. Ine ndinati, "Inu muli bwanji, dona?" Ndipo amuna awiri aja anali atapita ku chimbudzi. Ndipo iwo. . . Iye anali atakhala pamenepo, akuchita chidikhodikho, inu mukudziwa, akuseka. Botolo la kachasu litaikidwa pa tebulo, kapena mowa, uwo unali, zolezeretsa zitaikidwa apo, pomwe iwo anali kumwa. Ine ndinayenda kupita apo. Ine ndinati, "Inu muli bwanji?"

Ndipo iye anati, "O, moni."

Ndipo ine ndinati, "Kodi ine ndingakhale pansi?"

Iye anati, "O, ine ndiri ndi wondichezetsa."

Ine ndinati, "Ine sindimatanthauza izo mwanjira imeneyo, mlongo."

Iye anayang'ana pa ine pamene ine ndinamutcha iye 'mlongo.' Iye anati, "Kodi inu mukufuna chiani?"

Ine ndinati, "Kodi ine ndingakhale pansi apa miniti yokha."

Iye anati, "Dzithandizeni nokha." Ndipo ine ndinakhala pansi.

Ine ndinamuuzza iye zomwe zinachitika. Iye anati, "Dzina lanu ndi ndani?"

Ndipo ine ndinati, "Branham."

Iye anati, "Kodi inu ndi bambo muli kumusi uku mu malo amjaha awa?"

Ine ndinati, "Inde, mayi."

¹⁹⁵ Iye anati, "Ine ndakhala ndikufuna kuti ndibwere kumusi uko." Iye anati, "Bambo Branham, ine ndinaleredwa mu banja la Chikristu." Iye anati, "Ine ndiri ndi asungwana awiri aang'ono

omwe ali Akhristu. Koma zinthu zina, zinazake zinachitika, ndipo iye anafika pa njira yolakwika, kapena anayamba.”

¹⁹⁶ Ine ndinati, “Koma, mlongo, ine sindikusamala, Magazi akadali apobe kwa inu. Dziko ili liri lophimbidwa ndi Magazi.” Ngati Ilo likanati lisatero, Mulungu akanatipha ife, aliyense. Iye... Pamene Magazi amenewo achotsedwa, muyang’anire chiweruzo. Koma tsopano, ngati inu muti mufe wopanda Magazi amenewo, inu mupita kudutsa pa malo amenewo, ndiye uko kulibe chinthu choti chizichita mmalo mwanu. Lero Magaziwo akuchita mmalo mwanu. Ine ndinati, “Dona, zedi, Magazi akukuphimbaniwe inu. Utali wonse womwe inu muli ndi mpweya mu thupi lanulo, Magazi akuphimbani inu. Koma tsiku lina pamene mpweya udzachoka kuno, solo nitulukamo, inu mudzapita kudutsa Magazi amenewo, ndipo uko kulibe chinanso koma chiweruzo. Pamene inu mukadali ndi mwayi wa chikhululukiro...” Ndipo ine ndinamugwira iye pa dzanja.

¹⁹⁷ Iye anali akulira, anati, “Bambo Branham, ine ndikumwa.”

¹⁹⁸ Ine ndinati, “Izo sizimapweteka. Chinthu china, chimzake chandichenjeza ine kuti ndibwere kudzakuzani inu.” Ine ndinati, “Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko, anakuitanani inu, mlongo. Ndipo inu mukuchita molakwitsa, ndipo inu mukungozipanga izo moyipira.”

¹⁹⁹ Iye anati, “Kodi inu mukuganiza kuti Iye angandilandire ine?”

²⁰⁰ Ine ndinati, “Mwamtheradi, Iye angakulandireni inu.”

²⁰¹ Apo pa maondo ake, ife tinafika pansu pakati pa bwalo ilo, ndi msonkhano wachikale wa pemphero. Wa polisi uja anavula chipewa chake ndipo anagwada pa bondo limodzi. Apo ife tinali ndi msonkhano wa pemphero, mu malo amenewo. Bwanji? Mulungu ndi wochita mwayekha.

“Poika kumbali ntchito zakufa izi, tiyeni ife tipite mpaka ku ungwiro.”

²⁰² Tiyeni tisunthire mpaka ku malo awo komwe izi, “Ine ndine wa mu mpingo; ine ndine wa *uwu*,” izo zonse zatha. Ndipo tiyeni tipite mpaka ku ungwiro.

²⁰³ Mzanga wochimwa, ngati inu muli opanda Magazi lero, opanda chipulumutso, opanda chisomo, Magazi a Yesu Khristu akukugwirani inu. Inu mukuti, “Chabwino, ine zakhala zikundiendera nthawi yonse iyi.” Koma tsiku lina inu mudzapita komwe kulibe china chotsalira kwa inu apo.

Tiyeni ife tipemphere tsopano, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

²⁰⁴ Kodi alipo, angati akhale, mmodzi pano lero akanafuna kunena, “Mulungu khalani achifundo kwa ine, ine ndikuzindikira kuti ine ndachita molakwika”? Mwinamwake inu munajowina mpingo. Izo ndi zabwino. Koma ngati inu

simunalandire chisomo cha Khristu, kodi inu mungakweze dzanja lanu ndi kuti, “Ndipempherereni, ine, M’bale Branham”? Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, dona. Uko ndi kulondola. Musati... Mulungu akudalitseni inu, bwana, kumbuyo uko. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu. Kumbuyo komwe mmbuyomo, inde, Mulungu akudalitseni inu. Kwezani dzanja lanu. Ndiko kulondola. Ingokwezani dzanja lanu mmwamba, ndi kuti, “Mulungu, ndichitireni ine chifundo.”

²⁰⁵ Inu mukuti, “Ine ndine wa mu mpingo, M’bale Branham. Inde, i—ine ndayesera kuti ndikhale wabwino, Koma ine sindikudziwa, ine ndikungowoneka, zikuwoneka ngati, ine sindingakhoze kuchita izo.” O, mwendamnjira wosauka, mzanga wofooka wosauka, iwe ndithudi suwanawawonebe masomphenyawo.

²⁰⁶ Inu mukuti, “Mbale Branham, ine ndinafuula. Ine ndinayankhulapo ndi malirime. Ine ndinachita zonse izi.” Izo zikhoza kukhala zoon, aponso. Izo zonse ndi zabwino, palibe choti ndinene motsutsa izo.

Koma, mzanga wokonedwa, wotaika, koma, kuyankhula ndi malirime, kapena kugwedezeke, kapena kugwirana chanza, kapena kukhala wobatizidwa, izo, izo zonse nzabwino. Koma, kumudziwa Iye, ndi kumudziwa Munthuyo. “Kumudziwa Iye ndi Moyo.”

²⁰⁷ Inu mukuti, “Ine ndikulidziwa Baibulo, mwabwino kwenikweni.” Chabwino, kulidziwa Baibulo, si Moyo. “Kumudziwa Iye,” puronauni yaumwini, “kumudziwa Iye, Khristu,” kuti inu mukudziwa Iye wakukhulukirani inu.

Kodi inu mungangokweza manja anu, kachiwiri, wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu cha apa, m’bale. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, mnyamata waung’ono. Mulungu akudalitseni inu cha apa, mlongo. Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo komwe mmbuyo, uko. Ndiko kulondola. “Kumudziwa Iye, ndiwo Moyo.”

“M’bale Branham, mundikumbukire ine. Ine ndiri tsopano, pomwe pano mu mpando wanga, ndikuti ndimulandire Khristu.”

²⁰⁸ Nenani, “Bwerani mu mtima mwanga, Ambuye Yesu, ndi kupereka kwa ine mtendere uwo, kukoma uko.” Kupita ku mpingo, kukasewera zing’wenyeng’wenye zolimba monga inu mungathere, kuvina chokwera ndi chotsika, kuthamanga mkanjira, kupita kwanu mutalema, ndi kumakankhana ndi kukangana, zimenezo si Khristu. Inu mumapita ku mpingo, kukakhala ndi kumvetsera kwa ulaliki winawake wawung’ono wa momwe mlatho uti udzapakidwire utoto, kapena chinachake, chimzake monga choncho, osamvapo konse Mawu. Mawu

amabweretsa Moyo. Iwo ndi Mbewu. Kodi inu simukufuna mtendere?

²⁰⁹ Kodi inu mukusautsika ndi za kufa? Inu mukhoza kukhala ndi vuto la mtima lero, kodi izo zimakudandaulitsa inu? Kapena kodi inu mungasangalale, kuti, “Ine ndikupita kukakhala ndi Ambuye Yesu pa mapeto a msewu uwu?” Kodi inu mukumudziwa Iye? Ngati inu simuli, ingokwezani dzanja lanu. Ife tikuti tipemphe pemphero kwa inu. Inde, m’bale, inu, aponso.

²¹⁰ Chabwino, mu mtima mwanu tsopano.

Monga ndiri, wopanda chopempha,
Koma Magazi nakhetsera (ndani?) ine,
Poti ndilonjeza, nkhlupira,
Mwanawankhosa, Mwanawankhosa wa
Mulungu, ndidza. Ndidza, mofatsa,
mwachifundo.

Monga ndiri . . .

Ingoyendani kupita kwa Iye, mwa chikhulupiriro. Khulupirirani kuti Iye waima apo pomwe pambali ya inu. Iye ali.

. . .-ayi

Kuchotsa mmoyo wanga (mochuluka bwanji tsopano?) chimodzi . . . (kupsya mtima, njiru),

Kwa Yemwe Magazi Ake angayeretse banga,
O Mwanawankhosa . . .

²¹¹ “Mwa chikhulupiriro ine ndikuyenda kupita ku mtanda, mmawa uno. Ine ndikuika zolemetisa zanga pansu. Ine ndikubwera.” Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko. Ndizo zabwino. [M’bale Branham akuyamba kung’ung’uza *Monga Ine Ndiri*—Mkonzi.] Musakhale osayanjanitsika tsopano. Motentha, mokoma, yendani mpaka ku mtanda.

²¹² Mu Chipangano Chakale, iwo ankabweretsa mwanawankhosa. Iwo ankadziwa kuti iwo anachimwa, iwo ankadziwa izo mwa malamulo. Inu mukuzidziwa izo tsopano, chifukwa Mulungu wayankhula kwa mtima wanu. Iwo anali kuyang’ana pa malamulo, “Iwe usati uzichita chigololo. Iwe usati uzichita *zakuti-n-zakuti*.” Ndipo iwo ankatenga mwanawankhosa, ankapita ndi kukaika manja awo pa mwanawankhosa, wansembe ankadula khosilo. Kanthu kakang’onoko kankakankha, ndi kuukha magari, ndi kulira, ndi kufa. Manja ake ankakhala onse ataphimbidwa ndi magari. Mwanawankhosa ankafa mmalo mwake, koma iye ankachoka apo ndi chikhumbo chomwecho kuti akachichite izo kachiwiri.

²¹³ Koma mu malo awa, ife timabwera mwa chikhulupiriro, kudzera mu chisomo. Mulungu atatiitana ife. Iye timaika manja athu pa mutu wa Mwanawankhosa wa Mulungu. Iye timamva nyundo yozunguzidwa iyo. Iye timamva Liwu lija, “Ine ndiri ndi

ludzu; ndipatseni Ine okumwa. Atate, musawerengere tchimo ili kwa iwo; iwo sakudziwa zomwe iwo akuchita.” Mukuona? Mwa chikhulupiriro, ife timaimverera imfa Yake apo mmalo mwathu. Pansi pomwe mu mtima mwathu mumabwera mtendere wakuya, wokhazikika, pamene Liwu limati, “Iwe wakhululukidwa tsopano. Pita ndipo usakachimwe kenanso.” Momwe, mwa chisomo, ndiye, ife timachokapo opanda chilakolako chomwe chija, koma chikhumbo choti tisakachimwe kenanso kapena kukachita cholakwika chirichonse. Mtendere umene umadutsa kumvetsa konse, utalowa mu mtima mwathu.

Inu mutaulandira Iwo tsopano pamene ife tikupemphera, aliyense, palimodzi.

²¹⁴ Atate Akumwamba, iwo akubwera mwa chikhulupiriro, kudzera mu chisomo. Alipo pafupi manja khumi ndi awiri apita mmwamba. Izo ndi zipatso za Uthengawu. Iwo akubwera kwa Inu. Iwo akukhulupirira. Ine ndikukhulupirira mwa iwo, inenso, Ambuye. Ine ndikukhulupirira kuti, moonadi, Mzimu Woyera wayankhula kwa iwo. Ndipo mwa chikhulupiriro iwo akubwera kumene chokwera makwerero a Yakobo tsopano, mmwamba kumene mpaka pa phazi la mtanda, apo akuika pansi machimo awo onse, ndipo akuti, “Ambuye, izo ndi zondichulukira kwambiri ine. Ine sindingakhoze basi kunyamula izo motalikiranso. Ndipo kodi Inu mungandichotsera ine mtolo wanga wa tchimo, ndi kundichotsera chikhumbo kuchokera mu mtima mwanga kuti ndizichita chomwecho? Ndipo ndiloleni ine, mwa chikhulupiriro, tsiku ili, ndikulandireni Inu ngati Mpulumutsi wanga wanga. Ndipo kuyambira apa mpakana, ine ndizikutsatirani Inu mtunda uliwonse wa ulendowu, mpaka kumapeto a ulendowu. Ine ndagwira kuthwanima kwa chimene chimatanthauza ‘kupitirira mpaka ku ungwiro,’ osati kupita mu mpingo, ndi mizu ya ntchito zakufa monga ubatizo ndi zina zotero. Koma ine ndikufuna kuti ndipitirirebe, mpaka ine ndisakhaleponso, ndipo Khristu azikhoza kumakhala moyo mwa ine.”

²¹⁵ O Yesu, perekani izi kwa moyo wolapa uliwonse, mmawa uno. Aliyense yemwe anakweza manja ake adzalandire Moyo Wamuyaya chifukwa Inu munalonjeza izo. Iwo apanga kuvomereza kwapagulu. Iwo anakweza manja awo. Iwo anaswa malamulo onse okokera pansi. Iwo anaipanga sayansi kuti idzichitire manyazi kwayokha, chifukwa sayansi imati, “Mikono yako imayenera izigwera pansi.” Chirichonse chingatsimikizire izo mu sayansi, kuti iyo imayenera izikhala yomka pansi, chifukwa mphamvu yokokera pansi imaigwirira iyo pansi. Koma munali mzimu mwa iwo womwe unapanga lingalirolo, ndipo iwo ananyozetsa malamulo a mphamvu yokokera pansi ndipo anakweza manja awo. Inu munaziwona izo, Ambuye. Inu munaika dzina lawo pa Bukhu. “Akhululukidwa.” Bukhu lakalelo labwerera mu Nyanja ya Kuiwalira tsopano, sizidzati

zidakumbukiridwe kenanso. Aloleni iwo apite patsogolo lero, ngati Akhristu achikondi, okoma, kuti akakutumikireni Inu. Ndipo mwinamwake ambiri omwe sanakweze dzanja lawo, perekani kwa iwonso.

²¹⁶ Lolani oyera ayende moyandikira pang'ono, Ambuye, pakuti ife tiri tsiku limodzi pafupi ndi Kwathu kuposa ndi momwe ife tinaliri dzulo. Inu mukhale ndi ife, Ambuye, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu ndi kwa ulemerero Wake. Amen.



BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org